


NJIRA YA MNENERI WOONA

 Zikomo inu, M'bale Borders. Tiyeni tikhale chiyimire pamene tikukhala ndi pemphero. Ine ndikudabwa ndi ndani ali ndi chopempha usikuuno, mungakweze mmwamba manja anu ndi kunena, “Ambuye, ndi ineyo”? Tsopano tiyeni tiweramitse mitu yathu.

² Atate athu Akumwamba, monga ife tikumvera nyimbo imeneyo, “Ambuye, ine ndikukhulupirira.” Ife tikhoza kuganiza za—za nthawi zimene, kuzungulira dziko lapansi, ine ndaimvapo iyo mu zinenero zambiri, “Ambuye, ine ndikukhulupirira.” *Kungo Khulupirira*. Ndipo, Atate, ife tikupemphera kuti iyo ikhale yoposa nyimbo kwa ife usikuuno ndipo ikhale chenicheni. Mulole ife tikhale ndi chikhulupiriro chachikulu mwa Inu usikuuno.

³ Ndipo tsopano ife tikupempherera mpingo wawung'ono uwu, m'busa wake, M'bale wathu Fuller, wantchito Wanu, m'bale amene ife timamudalira. Ndipo ife tikupempherera banja lake, antchito ake pano, madikoni, matrasti, ndi onse amene abwera mu zitseko zopatulika izi. Ife tikupemphera, Ambuye, nthawizonse izikhala nyumba yowunikira ya Yesu Khristu.

⁴ Adalitseni abale onse otumikira amene ali pano usikuuno, iwo amene abwera mkati ndi kunja ndi ife, mnjira yonseyi. Ife tikupemphera, Atate, kuti Inu muwadalitse iwo mochuluka.

⁵ Ndipo ife tikupempha, usikuuno, kutsanulira kwina kwa Kukhalapo Kwanu pa ife. Ndife osowa, Ambuye. Ife tikukusowani Inu. Ife mosalekeza timakhala osowa chifukwa ife tiri pano pa bwalo la nkhondo, Ambuye, kumene zisankho zikuyenera kuti zipangidwe. Ndipo tikupemphera, Atate, kuti Inu mosalekeza mutilimbikitse ife ndi Kukhalapo Kwanu. Izo zimachita zochulukwa kwambiri kwa ife, kudziwa kuti Inu muli nafe. Mungodziwonetsera Nokha kuti mulipo, Ambuye, ndiye izo zitilimbikitsa ife kuti tizisunthira chitsogolo. Muchiritse odwala ndi osautsika. Mupulumutse otayika. Mulimbikitse okhumudwa. Muzitengere ulemelero kwa Inumwini. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

Inu mukhoza kukhala.

⁶ Ine ndikukhulupirira anali Davide amene anati, “Ndinasangalala pamene iwo anati kwa ine, “Tiyeni ife tipite ku nyumba ya Ambuye.””

⁷ Billy ananena, kanthawi kapitako, anati, “Kodi inu simukukhala ngati mukutopa, adadi?”

⁸ Ine ndinati, “Inde. Ine ndakhala wotopa moyo wanga wonse.” Zinangofika pakuti ine ndinazolowera izo.

⁹ Ine ndinayamba kuganiza, “Chabwino, ine ndikukalamba kwambiri. Ine ndikuyenera kukhala ngati ndikulekerera pang’ono.” Kenako winawake anadzabwera, pafupifupi wa usinkhu wa zaka eyite kapena nainte, akungotentha dzikolo, pafupifupi kawiri usinkhu wanga, inu mukudziwa. Ine ndinaganiza, “Mai! Ndikuzichitira ndekha manyazi.”

¹⁰ Kumusi ku kachisi kwathu, kuli banja laling’ono lachikale lotchedwa Kidd, amabwera kumeneko kuchokera ku Ohio. Tsopano, iwo awiri onse ali mu, chabwino mmenemo, eyite-faivi kapena eyite-eyiti. Ndipo iwo ndi okalamba kwambiri mpaka iwo sangathe kupita ku matchalitchinso mochuluka, chifukwa chawo...Iwo alibe mawu okwanira. Koma inu mukudziwa chimene iwo amachita? Pafupifupi tepi iliyonse...Mayi wachikulire uyu anasunga ndalama zake ndipo anagula tepi rekoda. Ndipo chotero iye amatenga tepi. Ine ndimamutumizira iye matepi. Ndipo iye amatenga matepi awa, ndipo iye amapita kuzipatala, kulikonse kumene iye angathe amakayika tepi rekoda iyi, iye ndi mwamuna wake wamng’ono wachikulire, amakasewera matepi amenewo. Kenako ndimamutumizira iye mpukutu wawukulu wa—wa nsalu za pemphero zimene ndazipempherera. Ndipo kamodzi kalikonse mu nthawi, “M’bale Willy, nsalu za pemphero zanditheranso.” Ndiyeno pamene ndiwawona iwo, iye amabwera mu tchalitchi, tsitsi laling’ono loyera, shawelo yaying’ono; ndi iye, mwamuna wamng’ono ndithu.

Pafupifupi zaka foro kapena faivi zapitazo, pamene ine ndinali ku...

¹¹ Kodi dzina la malo aja ndi chiyani uko ku Ohio, kumene amakhala ndi msonkhano umenewo chaka chirichonse? Iwo amawatcha iwo Chautauqua. Koma ine ndaiwala tsopano. Ndi pa bwalo kumeneko. Koma a—dzina la mzindawo ndi chiyani, ine ndikulephera kuwaganizira iwo. [M’bale akuti, “Franklin.” Mlongo akuti, “Miami, pafupi ndi Middletown.”—Mkonzi]. Tsopano, ndizo, inu mwatsala pang’ono tsopano. Winawake anati timayenda kudutsa Miami. [M’bale akunenanso, “Franklin.”] Ndipo iwo ndi pafupi ndi Franklin. Inde. Uko nkulondola. Pomwepo mu...Ine ndikukhulupirira ndi pakati pa Franklin...[Abale awiri akuti, “Middletown.”] Middletown. Ndi choncho. Uko nkulondola. Chotero, uko nkulondola, Middletown, kumusi pa mtsinje, chotero pa bwalo la Chautauqua kumeneko. Ndiro bwalo lalikulu limenelo la basiketibo, malo a masewero othamanga kumeneko.

¹² Ndipo m’bale uyu, oh, ine ndawadziwa iwo kwa zaka, ndipo M’bale Kidd wamng’ono wachikulire ali, oh, ine ndikuganiza iye anali eyite pamene anamutengera iye kumeneko, ndipo madokotala anapeza kuti matumbo ake anali atasanduka chotupa. Ndipo chotero chotupa ichi chinangomukutira iye. Chabwino, iwo anati icho chimayenera kupangidwa

opareshoni. Chotero pamene iwo anamutsegula iye, “Bwanji, panalibe chifukwa chomupangira opareshoni. Iye wapita kutali kwambiri.” Mukuona? Anati, “Palibe njira yochitira izo, nkomwe.” Chabwino, anamubweretsa munthu wamng’onyo kunyumba. Ndipo, opareshoniyo, yovutirapo pa bambo wa usinkhu wa zaka eyite zakubadwa. Ndipo iye ankangolemera pafupifupi, oh, ine ndikuganiza, kuchepera mapaundi handirede.

¹³ Chotero, Akazi a Kidd anayimba, kumeneko. Ine ndinali nditangobwera kumene kwathu kuchokera kwinakwake. M’bale Kidd anali akufa. Ndipo anati, “Iye akufuna akuwoneni inu, M’bale Branham, inu musana... iye asanachoke.” Chabwino, Billy ndi ine tinatembenuka. Ife tinalandira a—uthengawo, usiku wina, pafupifupi teni koloko. Ife tinanyamuka, mmawa wotsatira, pafupifupi foro. Chifukwa, masana tsiku lotsatira, ndinkayenera kuchokanso. Ndipo ife tinatsala pang’ono kung’amba matayala a galimoto yathu, tikukwera kumtunda kumeneko.

¹⁴ Mwamuna wokalamba wamng’ono, iwo anamudzutsa iye pamene ine ndinafika kumeneko. Ndipo iye anali ndi shawelo yaying’ono pamapewa ake, atakhala pamenepo ngati mbadwa yakale. Izo zinangochita chinachake kwa ine. Ndipo pamene ine ndinapita kuti ndikayang’ane pa iye, iye anayang’ana pamenepo.

¹⁵ Pamenepo panali dona wina wachikulire atakhala pamenepo, anali mmodzi wa mamembala a mpingo wake kuyambira pamene iye ankalalikira mmapiri, dziko la malasha mu Kentucky, kumene iye ankachapa kwa masenti fifitini pa tsiku, kuti amutumize mwamuna wake ku minda kuti akalalikire Uthenga. Zimenezo zinali pafupifupi zaka teni ine ndisanabadwe; akulalikira Uthenga! Ndipo iye anayang’ana kumeneko, ndipo iye anamutchula iye “agogoakazi,” ndipo iye wausinkhu wa zaka eyite. Ndipo iye anali atadutsa nainte. Ndipo chotero iye anati, “Agogoakazi, mukuwoneka oyera ngati chipale.”

¹⁶ Ine ndinaganiza, “Ndi mmene mtumiki ayenera kuyang’anira pa ena a osonkhana ake, atagona, atakhala pamenepo, akufa. ‘Agogoakazi, mukuwoneka woyera ngati chipale.’” Eya.

Ndipo iye anayang’ana mmbuyo pamenepo. Iye anati, “M’bale Branham?”

Ine ndinati, “Inde, M’bale Kidd?”

¹⁷ Iye anati, “Chabwino, ine ndikuganiza sipatenga nthawi kuti Iye atumize galeta wanga.” Anati, “Ine ndikupita, mmawa uno.”

¹⁸ Ndipo ine ndinati, “Zopambana, M’bale Kidd.” Ine ndinati, “Umo ndi momwe mukuyenera kumverera.”

¹⁹ Ndipo Mlongo Kidd wachikulire wamng’ono, ndi angati amamudziwa iye, muno? Eya. Ine ndikudziwa, oh, ambiri a inu mukumudziwa iye. Chotero iye anati. . . Iye anati, “Koma, M’bale Willy, kodi inu simukuganiza kuti Mulungu akhoza kuwachiritsa bambowo tsopano?”

Ndinati, “Ndithudi, Iye akhoza.”

²⁰ Ndipo iye anati, “Chabwino, ulemelero kwa Mulungu!” Iye anati, “Ngati Iye akufuna kundichiritsa ine,” anati, “Ndine—ndine wokonzeka kuti ndigwire ntchito kachiwiri.”

Ine ndinaganiza, “Usinkhu wa zaka eyite!”

Ine ndinayamba kugwada pansi. Pamenepo panabwera masomphenya. Zinali zimenezo.

²¹ Patapita masiku awiri, anamutengeranso iye ku chipatala. Anyamata ake ankagwira ntchito ku polisi uko mu mzinda. Iwo samamvetsa izo. Anamutengeranso iye kubwerera kwa adokotala. Ndipo dokotala anakanda mutu wake, anati, “Amuna, palibepo chomwe ndingapeze paliponse, tsopano, ndiwuzeni ine nkhani yanu.” Ndipo kenako iye ngati kuti agwetse chipatalacho. Anabwerera ndi tepi rekoda yake, apa iye anabwera, kudzasewera Uthenga. Ndipo iwo amakhala uko ku. . . Ndipo kumeneko pafupi ndi Chautauqua ndi kumeneko.

²² Tsopano, mwamsanga ine ndikangoyamba *Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri*, monga ife tinachitira *Mibadwo Isanu Ndi Iwiri Ya Mpingo*. Iye anandiyimbira ine foni usiku wina, iye anati, “Chabwino, wokonedwa, ngati ndikanangokhala ndi ndalama,” iye anati, “Ine ndithudi ndikanakonda kuti ndibwere kumeneko.”

²³ Ine ndinati, “Iwalani zimenezo, Akazi a Kidd. Chanu—chipinda chanu chikudikirira. Inu ndi abambo mubwere kuno.”

Iye anati, “Adalitse mtima wanu wawung’ono!”

²⁴ Ndipo izo zimagondipangitsa ine kumverera bwino kwenikweni, inu mukudziwa, chifukwa iwo amandilimbikitsa ine. Pa usinkhu wa zaka eyiti-faivi kapena eyite-sikisi, ndipo akupitabe. Ndiye ine, nkumadandaula kuno, pa fifite-firii. Chotero, mai, izo zimakupangitsa iwe kumverera ngati ulimbe mtima.

²⁵ Chabwino, ife tiri ndi zambiri zoti tikambe, ndipo gulu lokoma chotero kuliyankhula, bwanji, ife tikhoza kungokhala pano theka la usiku.

²⁶ Koma inu mukuyenera kupita ku Sande sukulu mmawa tsopano. Tsopano, inu muyenera kukhala wotsimikiza kuti muchite zimenezo. Ndipo kumbukirani, ine nthawizonse ndimati, ndi tchimo mwamtheradi kuwatumiza ana anu ku Sande sukulu. Musamachite konse zimenezo. Izo ndizolakwika. Muziwatenga iwo, nthawizonse. Mukuona? Nthawizonse muzipita nawo. Iye. . . Ndipo chotero, tsopano, umo ndi mmawa.

27 Chotero, tsopano, ngati inu munayenera kuti mujombe ku ntchito, kuti mudzamve, kuti mudzakhale ndi ife ndi kudzapemphera nafe, ndi zina zotero, inu mukuyenera kujomba ku ntchito, izo ziri bwino. Mungopitirira ndi kujomba ku ntchito, koma musajombe ku tchalitchi. Musamajombe ku tchalitchi. Ine sindingakuchedwetseni kuti mujombe ku tchalitchi. Koma ngati mukuyenera kujomba ku ntchito, kamodzi pakanthawi, izo zizingapweteke. Tsopano, chifukwa, ntchito, ndi mkate wanu wa tsiku ndi tsiku, ndipo, inu, Ambuye analonjeza kuti adzakupatsani zimenezo. Chotero, koma, ichi, inu mukuyenera kukhala otsimikiza kwenikweni kuti mubwere ku tchalitchi. Inu mukuwona?

28 Ine ndikuganiza, mawa mmawa, ine ndidzakhala ndi m'bale wina wabwino kuno mu mzinda. Koma sindikudziwa kuti dzina lake ndi ndani tsopano. Ine ndikuganiza iwo umatchedwa Mpingo wa Apostolic, kapena Mpingo wa Apostolic, kani. Ndi Mpingo wa Apostolic. Ine—ine ndikhoza kumudziwa m'baleyo. Dzina lake siliri pa pepala. Koma ine—ine sindikudziwa kuti m'baleyo ndi ndani pa nthawi ino. Kenako mawa usiku, uko... [M'bale akuti, “Macias.”—Mkonzi]. Pepani? [“M'bale Macias.”] M'bale Macias. Oh, Macias. Oh, mpingo waku Mexico. Nkulondola uko? Oh, kodi ameneyo ndi amene anamtenga malo a M'bale Garcia pamene iye ankachoka kuno? [“Kulondola.”] Chabwino. Izo ziri bwino kwambiri.

29 Titi, ine ndinalandira kalata, kuno nthawi yina kalelo, yochokera kwa mwana wake wamkazi, uko... M'bale Garcia, kumtunda ku—ku California, akugwiritsitsabe. Chotero, ndine wothokoza kwambiri. Ndipo ine ndinamuwona M'bale ndi Mlongo Garcia pamene ine ndinali ku San Jose, ine ndikukhulupirira, ndi M'bale Borders kumtunda uko. Iwo ali bwino basi. Ine sindidzayiwala konse mausiku amenewo kumeneko ku mpingo wawung'ono waku Mexico umenewo. Ine sindinamvepo zambiri za “Gloria a Dios” mmoyo wanga wonse. Ine sindidzaiwala konse zimenezo, “Gloria a Dios.”

30 [M'bale Williams akuyankhula ndi M'bale Branham—Mkonzi]. Mai! Zikomo inu, M'bale Williams. Izo nzabwino. Mipando fifitini handiredi, mmawa, mu tchalitchi chino. Titi, aliyense abwere, ngati inu simupita... Tsopano, dikirani miniti. Ine kulibwino ndikhale osamala za izo. Ine ndinanena chinachake cholakwika ndiye. Ayi. Kuwona mtima konse, inu muli pa malo anu antchito. Mukuona? Musatero... Tsopano, izo zonse ziri bwino.

31 Ndipo lero ndinapeza kuti iwo... Ndinawona hema. Ine ndinali kumusi kuno ku Sixteenth and Henshaw. Kapena, ndicho chimene chinali pamene ine ndinali mu, kuno mu Arizona, pafupifupi zaka sarte-faivi zapitazo, msewu wakale wafumbi. Ine ndinapita kunja uko kumene iwo anali, ndipo iyo inali Sixteenth and Henshaw. Ine ndinkakhala

kumeneke ndi anthu ena, Francisco, ndipo—ndipo tsopano inu simungawadziwe malo omwewo. Mpaka anasintha dzinalo. Ine ndikuganiza kuti kukumatchedwa Buckeye Road tsopano.

Ndipo, oh, momwe zinthu zimasinthira, koma Mulungu samasintha.

³² Ndipo chotero ine ndinali kumeneke ndipo ndinawona kuti m'bale ali ndi msonkhano wamu hema. M'bale wina kumusi uko amene wamanga hema. Ine ndinazungulira kuti ndiwone ngati ndingamuwone iye, koma sindinamuwone iye paliponsepo, kuti ndimuuze iye kuti sitinali kuno kudzapanga mpikisano ndi iye. Koma, kungoti kuli anthu ambiri kuno!

³³ Ine ndikumukumbukira Jack Shuler. Izi zingakhale zabwino kwa inu Amethodisti. Pamene ine ndinabwera kuno nthawi yina, ndinali ku Madison Square Garden, Jack anali kunja kuno ku—ku sukulu ya sekondare. Ndipo—ndipo ndinamumbira iye. Ndipo ine ndinati, “M'bale Jack?”

Iye anati, “Inde. Kodi ndi M'bale Branham?”

Ine ndinati, “Inde.” Ine ndinati, “Ine ndikukulowererani inu kuno.”

³⁴ Ndipo iye anati, “Ayi.” Anati, “Ayi. Ine ndinangokhala motalika kwambiri ndipo ndinalowa mu nthawi yanu.”

³⁵ Ndipo ine ndinati, “Oh, ine ndikupepesa, M'bale Jack.” Ine ndinati, “Ine sindinati. . .”

³⁶ “Ah,” iye anati—anati, “izo ziri bwino, M'bale Branham.” Anati, “Iwo amangofuna kuti ine ndikhalebe.”

³⁷ Ine ndinati, “Oh, gulu langa silikuvutitsani inu kunja uko, mulimonse, Jack,” ine ndinati, “chifukwa pafupifupi anga onse ndi Achipentekoste.”

Iye anati, “Ndithudi, anga ali, nawonso.”

Ine ndinati, “Eya?”

“Bwanji,” iye anati, “ndithudi.” Iye anati, “Ndine wa pentekoste.”

³⁸ Ine ndinati, “Tsopano, kulibwino inu musamudziwitse Bob zimenezo.” Ndi abambo ake, inu mukudziwa. Ndipo iwo ndi a Methodisti, nawonso, olochedwa mu ubweya, inu mukudziwa.

³⁹ “Chabwino,” iye anati, “M'bale Branham, kodi inu simukudziwa chimene wa—pentekoste ali?”

Ine ndinati, “Ndikuganiza chomwecho.”

Anati, “Ndi Orthodox Methodisti.”

⁴⁰ Uko nkulondola basi, Orthodox Methodisti. Uko nkulondola. Ngati mpingo wa Methodisti ukanapitirizabe ndi uthenga wake, iwo ukanapitirira mpaka mu pentekoste. A—Mpingo weniweni unatero.

⁴¹ Ayi, osati kunyozetsa chipembedzo chanu tsopano, m'bale. Mukuona? Chifukwa, pentekoste si bungwe. Iwo anayetsa kuchita zimenezo, koma iwo ndithudi alephera mu izo. Mukuona? Ndi chokuchitikira. Eya. Pentekoste ndi ya Akatolika, kapena—kapena Ayuda, kapena aliyense amene amapeza. . . Pentekoste ndi chokuchitikira, osati bungwe.

⁴² Ndipo tsopano ngati aliyense ali ndi Baibulo lanu lotsegula, kapena pafupi, kuti mukufuna kuti muwerenge nane Mawu pang'ono. Ine ndimakonda kuwerenga Mawu, sichoncho inu? Chifukwa, kuwonjezera apo, chimene ine ndinganene chikhoza kulephera, chifukwa ndine munthu. Koma chimene Iye amanena sichingalephere. Mukuona? “Miyamba ndi dziko lapansi zidzachoka, koma Mawu Anga sadzalephera.” Oh! Kodi izo sizodabwitsa? Mawu Ake sadzalephera konse. Ndi chinthu chaulemelo bwanji chimenecho! Mawu Ake sadzalephera konse.

⁴³ Tsopano tiyeni ife tiwerenge usikuuno kuchokera, ndi kutenga nkhani yaying'ono kuchokerapo, imene ine nditi nditenge ngati mutu, Ambuye akalola. Iyo ili mu Bukhu la Amosi, ulosi wa Amosi. Ndipo iye anakhala pafupifupi seveni handirede ndi. . . Ndikuganiza kuti ndi zaka seveni handirede ndi eyite seveni Khristu asanabwere. Tiyeni titsegule ku mutu wa 3 wa Amosi, Mawu a Ambuye kudzera mwa Amosi. Ndipo ine—ine ndimamukonda mwamuna uyu. Iye amatengedwa ngati mmodzi wa aneneri aang'ono, koma iye ndithudi anali ndi Mawu a Ambuye.

Imvani mawu awa amene AMBUYE ayankhula motsutsa inu, O ana a Israeli, motsutsa banja lonse limene ndinalitulutsa mdziko la Igupto, ndi kuti,

Inu nokha ine ndakudziwani. . . mabanja onse a padziko lapansi: chifukwa chake ndidzakulangani chifukwa cha mphulupulu zanu zonse.

Kodi awiri angayende limodzi, asanagwirizane?

Kodi mkango ungabangule m'nkhalango wopanda nyama? kodi mkango wawung'ono ungaliye mdzenje muake, ngati iwo sunagwire kanthu?

Kodi mbalame ingakodwe mu msampha pa dziko lapansi, pamene palibe msampha wotcheredwa kwa iyo? kodi wina angatchere msampha padziko lapansi, osakola kanthu?

Kodi lipenga lingawombe mu mzinda, ndipo anthu osawopa? kodi mudzakhala choyipa mu mzinda, ndipo AMBUYE asanachichite icho?

Ndithudi Ambuye. . . sadzachita kanthu, koma iye amawulula zinsinsi zake kwa antchito ake aneneri.

*Mkango ukabangula, ndi ndani amene sawopa?
Ambuye MULUNGU wayankhula, ndani amene sanenera?*

44 Ambuye awonjezere madalitso Ake ku Mawu awa.

45 Maso ake aang'ono akuyenera kuti anawonda, pamene dzuwa lotentha linkawala mmawa umenewo ndi kunyezimira ndevu zake zoyera ndi tsitsi lake, pamene iye anakwera pamwamba pa phiri kumpoto kwa Samariya ndi kumayang'ana pa mzindawo. Zovala zake zinali zawamba, ndipo mapazi ake anali ndi fumbi. Iye analibe mawonekedwe, koma iye anali ndi PAKUTI ATERO AMBUYE kwa anthu.

46 Ndi zosiyana bwanji lero ndi uvangeri wathu wamakono! Ndi kakhazikitsidwe kosiyana bwanji kamene ife tiri nako, kumuposa iye!

47 Munthu wamng'ono uyu, si wina koma Amosi, mneneri woona wa Ambuye, ndi Mawu a Ambuye, kwa m'badwo wochimwa umenewo! Wopanda mantha uyu, munthu wamng'ono analosera mmasiku a Yeroboamu wachiwiri.

48 Yeroboamu anali wanzeru, wanzeru kwambiri, munthu wanzeru, koma iye anali wopembedza mafano. Ndipo Yeroboamu anali atatsogolera ufumu wake mpaka pachimake, koma iye anali mu kupembedza mafano. Iye anachita izo mwanjira yolakwika. Koma ufumuwo unali utachita bwino pansi pa Yeroboamu.

49 Ndipo, kawirikawiri, kulemera kumayambitsa tchimo. Anthu ambiri amayang'ana pa kulemera ngati madalitso. Izo zikhoza kukhala, ngati ife tingazigwire izo molondola. Koma kawirikawiri zimatsogolera ku tchimo, kusalemekeza Mulungu.

50 Ufumuwo unali ukuyenda bwino mu tsiku lake. Ndipo, anthu. Iye anali atapanga mgwirizano ndi mafuko onse omuzungulira iye.

51 Ndipo momwe Israeli anali ataseselekera ku tchimo loyipa, anachoka kwa Mulungu, anachoka ku malamulo Ake ndi malangizo Ake, ndipo anali atapita kutali, pamodzi, chifukwa cha kupsyantima. Akazi ankayenda mmisewu, atavala zovala zawo zabwino, zopanda ulemu. Amunawo ankayendayenda, akutchova juga ndi kumamwa. Nyumba zamu msewu, tingadzitche izo lero, malo azisangalalo, ataseguka kwambiri mu mzindawo.

52 Tchimo linkanyalanyazidwa ndi utumiki, ankangokhala otseguka. Malo okongola, malo abwino ochezera alendo, ndipo amakhala otsegula. Tchimo silinkadzudzulidwanso pa guwa. Ilo linali litamasulidwa.

53 Ndipo pamene ulosi uwu unabwerapo, iwo unkawoneka ngati iwo sukanati...Icho chikanakhala chinthu chotsiriza chimene chikanakhoza konse kuchitika. Malingana ndi chimene mneneri uyu ananena kwa iwo, icho chidzakhala chinthu

chotsiriza chimene chikanakhoza kuchitika kwa iwo, kutengera momwe iye anatemberera m'badwo umenewo. Koma, komabe, mu zaka fifite, ufumu wawo unafafanizidwa kwathunthu pa dziko lapansi.

⁵⁴ Mulungu amayankhula Mawu Ake. Ndipo Mawu a Mulungu ali ngati Mbewu. Ndipo pamene Iwo afesedwa, pamene mneneri ameneyo akubwera ndi Mawu a Ambuye ndi kuwayankhula mawu amenewa, iwo ankayenera kukwaniritsidwa, ngati iwo anali Mawu a Mulungu. Pamene a—Mawu a Ambuye ndi odzozedwa, ndipo Iwo ndi Mawu a Ambuye, Iwo akuyenera kutenga malo Ake mu nyengo Yake.

⁵⁵ Ife tikhocha kuwawona Iwo, patapita zaka masauzande, akutenga malo Ake lero. Iwo akuyenera kuchita izo, chifukwa Iwo ndi Mawu a Ambuye, ndipo Iwo sangawonongeke.

⁵⁶ Winawake amayankhula tsiku lina kwa ine, ndipo anati, “Genesis ndi yolakwika, ndipo masiku sikisi a kulenga, amene Iye ananena.”

⁵⁷ Ine ndinati, “Genesis 1 mpaka (Genesis) 2 ndi chinthu chosiyana mwamtheradi.” Mutu wa 1 wa Genesis umati, “Pachiyambi Mulungu analenga miyamba ndi dziko lapansi,” zathera pompo. Momwe Iye anachitira izo, ndi pamene Iye anachitira izo, izo ziri kwa Iye. Inde. Kenako, “Dziko lapansi linali lopanda mawonekedwe, ndi lopanda kanthu,” ndiye ife timayambira pamenepo, ku kulenga. Koma, “Pachiyambi,” motalika bwanji, ife sitikudziwa. Mbewu zonsezo zimene Iye anali nazo mmenemo pamene madzi anachoka, moyo unabwereranso pa dziko lapansi, zinadzazitsa dziko lapansi. Ndipo pamene Mawu a Mulungu afesedwa, palibe chimene chingawalepheretse Iwo kuchitika.

⁵⁸ Ndipo mneneri wamng'ono wopanda mantha uyu anachokera kosadziwika. Chinthu chokhacho chimene ife timawuzidwa, nehakuti iye anali wolishya ziweto. Sitikudziwa kuti abambo ake anali ndani. Sitikudziwa kuti amayi ake anali ndani. Sitikudziwa kumene aliyense wa mtundu wake, palibe chirichonse cha iye.

⁵⁹ Umo ndi momwe kawirikawiri anthu amene amatumidwa kuchokera kwa Mulungu amabwerera powonekera. Iwo amachokera kosadziwika, ndipo amadzazowa mwanjira yomweyo. Ife tinalibe mbiri ya iye, chimene chinachitika.

⁶⁰ Mwamuna wamkulu uyu Yeroboamu, yemwe anali a—woganiza mwamphamvu kwambiri, ndipo iye anali nalo fuko liri lolemera, komabe, mu tchimo.

⁶¹ Ine ndikudabwa, ngati sitingangofanizira izo pang'ono pokha usikuuno ndi dziko lathu lomwe, fuko lathu lomwe, mu tchimo momwe ilo liriri. Komabe, lolemera, atichosera msonkho, nthawi yomweyo, ndikumva choncho. Ndithudi, aliyense akhoza

kuwerenga pakati pa mizere pamenepo, chisankho chikubwera. Koma, zina zotero, zinthu zonsezi zimene zikuchitika.

⁶² Israeli, alaliki, ansembe, ndi boma anali atawasiya Mawu a Mulungu mmbuyo, ndi kumanyengerera. Ndipo ndi chifukwa chake dziko linali mu chikhalidwe chimene ilo linali, ngakhale iwo anali ndi ansembe ochuluka, ndi alaliki ochuluka basi monga iwo anayamba akhala nawo. Koma iwo anali atawasiya Mawu a Mulungu, anali atachoka kwa Iwo. Ndipo nthawizonse zimakhala pa nthawi imeneyo, pamene Mulungu amatumiza winawake kuchokera kosadziwika, kuti adzaphulitse izo kubwerera mu njira yake kachiwiri. Munthu wina wopanda mantha adzawuka ndi Mawu a Ambuye ndi kudzawagwedezera anthu ku Mawu kachiwiri.

⁶³ Ine ndimangowona apa. Ndinali nditalemba chinachake apa, chimene ine mwinamwake ndikanafuna kuti ndilozereko kachiwiri. Ndizo pa mutu wa 2, ndime ya 4. Ndikufuna kuti ndiwerenge iyo. Mvetserani kwa munthu wamng'ono uyu akuyankhula izi.

Pakuti atero AMBUYE; Chifukwa cha zolakwa zitatu izi za Yuda, ndi...foro, sindidzabweza chilangocho chotero; chifukwa iwo anyoza lamulo la AMBUYE, ndipo sanasunge malamulo ake, ndipo mabodza awo anawapangitsa iwo kulakwitsa, amene makolo awo anatsatira:

⁶⁴ Mukuona pamene uthenga wake unali? Kuwuyika iwo mmbuyo momwe, kuti iwo anali atachoka ku Mawu a Mulungu. Kwa wowerenga Baibulo aliyense, zimenezo zimakupangitsa iwe kudziwa kuti iye anali mneneri wona. Iye anawabwezeretsa iwo pa Mawu, pamene iwo anali atagwapo.

⁶⁵ Oh, mwinamwake mipingo yawo inali italemera. Iwo mwinamwake anali ndi nyumba zabwino. Mzinda wawo mwinamwake unali wokongola kwambiri kuposa Phoenix. Kunali ku Samariya, monga ife tonse tikudziwira, anali malo abwino oyendera alendo. Iwo akanali panobe, malo okongola.

⁶⁶ Koma, komabe, iwo anali atachoka kwa Mulungu. Ndipo Mulungu anatumiza wamthenga uyu kwa iwo. Ndi uthenga wa chidzudzulo bwanji wochokera kwa Mulungu! Mneneri wamng'ono uyu anawabweretsera iwo.

⁶⁷ Tsopano, Amosi anabwera kuchokera mchipululu, kupita ku mzinda wokongola. Nzosadabwitsa kuti maso ake aang'ono opatsidwa ndi Mulungu anawonda pamene iye anali pamwamba pa phirilo. Iye...

⁶⁸ Osati monga wodzawona malo angachitire, madona, kudzati, “Yang'anani pa zogula zonse zomwe amayi akuchita. Tayang'anani pa masitairo atsopano amene iwo ali nawo kumusi kuno,” kapena osati monga momwe ena a anthu angaganizire, “Ma kasino, ndi zina zotero, zinali zazikulu kwambiri mu

mzindawo,” kapena chifukwa chakuti iwo akhoza kukhala pa ngodya za msewu ndi kumayang’ana kudutsa kwa amuna kapena akazi, kumasilira.

⁶⁹ Koma mneneri uyu, maso ake anawonda chifukwa cha tchimo limene iye analiwona mu mzindamo. Samawonda chifukwa cha zinthu zimene ankazisirira, koma powona momwe iwo anali atatalikirana ndi Mulungu, anthu amene anayitanidwa ndi kusankhidwa. Kodi inu munazindikira apa? Iye anati, “Ine sindikudziwa anthu ena koma inu. Ine ndinakutulutsani inu mu Igupto, ndipo kenako inu mukuchoka kwa Ine monga chomwecho.”

⁷⁰ Ndipo pamene mneneri uyu, akubwera kuchokera kolishya mmbuyo uko ku dziko la kumpoto, ndi Mawu a Ambuye, momwe iye anayang’anira pa mzinda umenewo. Akuyenera kuti anapukuta thukuta. Zovala zake zinali zong’ambika. Ndipo mwinamwake analibe ndalama zokwanira kuti azigulire a—malo ogena a usiku umenewo. Izo sizinapange kusiñana kulikonse kwa iye. Iye anali ndi uthenga umene unali ukuyaka mu mtima mwake, ndipo iye ankayenera kuti awubweretse iwo. Osati chokhacho, koma kudzoza kwa Mzimu Woyera kumene kunamukantha iye mchipululu mmenemo, kunatseketsa maso ake ku kukongola kwa dzikolo.

⁷¹ Ndipo wantchito aliyense wodzozedwa wa Khristu, maso awo amachititsidwa khungu ku zinthu za mdziko. Iwo samaziwona zinthu zimenezo. Iwo samazifunafuna izo. Iwo amakhala ndi chinthu chimodzi: Khristu ali patsogolo pawo. Ndizo zonse zimene iwo amaziwona. Iwo samawopa kalikonse. Khristu ali patsogolo pawo. Uthenga ukuyenera kuti ukaperekedwe kwa anthu, ndipo iwo samayima pa kalikonse. Inu simungawuzimitse Iwo kuchoka mwa iwo. Inu mukhoza kuwayika iwo mu ukayidi, ndende, chirichonse chimene inu mukufuna. Iwo amatuluka mu izo kachiwiri. Ameneyo ndi wodzozedwa wa Ambuye. Inde.

⁷² Iye anayang’ana pa kuvunda kwauzimu kwa mzindawo, chivundi, ndi kuvunda kwauzimu kwa mzindawo.

⁷³ Ndikudabwa ndi antchito angati a Ambuye, akamawoloka pa phiri kumtunda kuno, angayang’ane pa Phoenix? Inu mumabwerera kuno chifukwa cha kukongola, ndi kuwala kwa dzuwa, ndi kudzapuma, zimene ife sitingayankhule mopepuza za izo.

⁷⁴ Kuno osati kale kwambiri, nthawi yomaliza imene ine ndinali kuno, nditakhala pa South Mountain, mkazi wanga wakhala kumbuyo uko, ine ndinali kuyankhula kwa iye. Ine ndinati, “Pafupifupi zaka firii kapena foro handirede chigwacho chinali malo okongola, sindikukayikira, pamene Mtsinje wa Salt unkadutsa kuno, ndi ankhandwe, ndi zina

zotero, ndi kuphukira kwa kaloga. Taonani momwe icho... Chinthu chonsecho chasanduka chisokonezeko cha tchimo.”

Ndipo iye anati, “Chabwino, ndiye nchiyani chimakubweretsa iwe kuno?”

⁷⁵ Ine ndinati, “Ndi ichi chimene chimandibweretsa ine kuno. Ngakhale mu mdima wake ndi mu tchimo limene liri mu mzindawu, alipo maumboni ena a Ambuye, zosedmedwa zamoyo za Khristu, kumusi uko. Ine ndimabwera kudzayika phewa langa ndi iwo, kuti ndidzawalitse Kuwala kwa Uthenga. Ena a abale aang’ono achikulire amenewo kumusi uko pa ngodya ya msewu penapake, anakonza izo, ndipo anatulutsa thukuta, ndi kulira ndi kupempherera izo, ali ndi uthenga pa mtima pawo. Ine ndimabwera kudzaponya gawo langa ndi iwo, kuti ndidzawalitse Kuwala kwa Uthenga wosayipitsidwa wa Yesu Khristu ku dera lalikulu la mzinda uno wa Phoenix.”

⁷⁶ Mmenemo, ngakhale, iwo akhoza kukhala malo odabwitsa; ngati munthu atangotenga zopindula zake zimene iye wakwanitsa kuzichita, kuti amange nyumba zokongola monga pamwamba pa Phiri la Camelback, Phiri la Cavalier. Pamene ndimadutsa kumeneko, bwanji, zaka sarte-faivi zapitazo, iwo anali chipululu. Tinkathamanga ndi abulu kudutsa kumeneko pa akavalo. Ndipo cha ku South Mountain kuno, kuthamangitsa abulu ndi akavalo.

⁷⁷ Ndipo tsopano lakhala dera lalikulu la mzinda wokongola uwu. Ilo likukula kukhala ma teni amasauzande kuchulukitsa masauzande. Ilo latambasulidwa, kufikira tsopano kuvunda kwa mizindayo kwawubweretsa iwo ku chipwirikiti. Utsi ukulowamo. Chinyezi chanu ndi choyipa monga momwe ziliri ku Jeffersonville, Indiana, mu Chigwa cha Ohio. Kuthirira... Munthu nthawizonse amayipitsa dziko. Pamene Amwenye anali nalo ilo, iwo anali malo okongola. Koma pamene mzungu anadzabwera, iye anadzabweretsamo machimo ake, ndi mowa, ndi chivundi. Ndipo iye wayipitsa mayikowo mpaka iwo sikanthu koma chithaphwi. Ndi chinthu chotani kuchiyang’ana! Mulungu adzalichotsapo ilo pa dziko lapansi, limodzi la masiku awa.

⁷⁸ Ndipo Iye akusankha anthu, mu chirungamo, amene ati adzalamulire pa dziko lapansi, pamene Iye azidzalamulira ngati Mfumu. Iye tsopano akuwatengera anthu Ake ku Dzina Lake, anthu aku Ufumu Wake.

⁷⁹ Tsopano, kodi gulu ili lanzeru, laluntha, laluntha la Israeli; purezidenti wake wamkulu, wamphamvu, waluntha kapena mfumu, Yeroboamu, amene anali munthu wanzeru; ndipo kodi iwo akanamumvera mneneri wamng’ono uyu, wosadziwika? Kodi uthenga wawukulu uwu, umene ukuyaka mu mtima mwake, kodi akanakwanitsa kumayenda mmisewu, ndipo anthu akanati, akazi akanakhoza, kudziveka okha

mwabwinobwinonso, amuna akanachoka mmathalaveni ndi malo a tchimo, ndi kutembenukira kwa Mulungu pa kulalikira kwa munthu wamng'ono, wosadziwika uyu? Limenelo linali funso likhoza kubwera mmalingaliro ake, kapena izo zimatero kwa ine, pamene ndikumuwona iye atayima pamenepo, ndipo mutu wake wawung'ono, wadazi ukuwala padzuwa. Ndevu zake za imvi zikulendewera pa chikhoto chake. Akuyang'ana pansi kudutsa pamenepo, ndipo akuyang'ana pa mzinda umenewo, ndi maso ake atawonda, ndipo mtima wake ukugunda.

⁸⁰ Ndipo komabe, mmenemo, iye ankawona Ufumu wa Mulungu, umene un kayenera kukhazikitsidwa mmenemo, zonsezo zitalemetsedwa mu tchimo. Ndipo ali ndi chidzudzulo chochokera kwa Mulungu, chimene chikanati chidzudzule kuchokera kwa mfumu mpaka kwa wopemphetsa mu msewu, wansembe aliyense, mlaliki, mfumu, wamphamvu, mfumu, chirichonse chimene iye anali, iye anali ndi themberero la Mulungu loti ayike pa iwo. Chifukwa iwo... Inu mukuganiza kuti iwo akanamulandira iye. Oh, iwo akanamvetsa izo?

⁸¹ Kumbukirani, iye analibe kuvomerezedwa. Iye anabwera mosiyana ndi avangeri athu a lero. Iye analibe kuvomerezedwa kuchokera kwa ansembe. Iwo sankadziwa nkomwe chimene munthuyo anali. Koma kunali Mmodzi amene ankadziwa yemwe iye anali. Ameneyo anali Mmodzi amene anatumama iye. Ndizo zonse zinkawerengedwa, kwa iye, bola ngati iye ankadziwa kumene iye anatumidwa. Uthenga wake un kayenera kuti uzipita mofanana basi, ndiponso mosalabadira.

⁸² Iye analibe zikalata za chipembedzo zoti zikamuthandizire iye pamene akupita mu mzindawo, kuti abwere ku bungwe la atumiki, kudzati, "Abale anga, ine ndatumidwa ndi gulu linalake *ili*, gulu lachipembedzo ili. Ine ndine wa *akuti-akuti*." Iye analibe zimenezo. Iye analibe chirichonse cha zinthu zimenezo. Komanso iye analibe khadi la chiyanjano kuti akawonetse kuti iye analinso mu chiyanjano chabwino ndi bungwe la atumiki ochokera kudziko limene iye ankachokerako. Iye analibe mgwirizano pa msonkhano wake. Iye sanamufunsire nkomwe aliyense za izo.

⁸³ Munthu wamng'ono ameneyo anali atayima pa malo ovuta. Zikanakhala zokwanira kwa munthu kuti atembenuke ndi kubwerera mmbuyo, ndi kukazitenganso ziweto zake, kukapitiriza pamene iye analekezera, ngati iye akanangoganizira.

⁸⁴ Koma, inu mukuona, bamboyo sanatenge lingaliro lachiwiri. Iye sanaganizire za ziyeneretso zirizonse, komanso sanaganizire za khadi la chiyanjano. Iye anangoganizira za chinthu chimodzi, ndipo amenewo anali Mawu a Ambuye. Mulungu anali atawapereka Iwo kwa iye ndi ulamuliro, kuti iye amayenera kupita kumeneko ndi kukanenera. Ndizo zonse

zimene zinapanga kusiyana kulikonse kwa iye. Iye anali ndi Mawu a Ambuye, ndipo chotero iye anamverera kuti samasowa zomuyenereza, kapena kuvomeredzedwa kulikonse, kapena mgwirizano uliwonse. Chinthu chokhacho chimene iye ankasowa, chinali, iye anali ndi mgwirizano ndi Mulungu, ndipo ndizo zonse zimene zinatengera. Bola ngati iye anali mu chifuniro cha Ambuye, kodi izo zipanga kusiyana kotani? Bola ngati iye ankadziwa kuti uthenga wake unali wochokera kwa Mulungu, Mulungu akanadzatsimikizira uthenga umenewo. Iye ankayenera kutero.

⁸⁵ Ndipo pamene iye anabweretsa uthenga, izo zikuwoneka ngati pakanakhala ansembe onse, ndi alaliki, ndipo aneneri a m'badwo umenewo, akanabwera ndi kudzalapa, chifukwa iwo akanawona chikhalidwe cha malowo, kuwona kuyipitsidwa kwa makhalidwe. Koma pamene iye anayamba kunenera ndi Mawu a Ambuye, Iwo anali achirendo kwa iwo. Iwo sankadziwa kanthu za Iwo.

⁸⁶ Ndi chithunzi ndithu cha izo lero. Wachilendo, uthenga wa Ambuye! Mpingo sukudziwa kanthu ka izo. Pamene iwo amva anthu akudzuka ndi kupereka uthenga mu malirime osadziwika, ndi kupereka kutanthauzira kwa iwo, ndi kunena kuti chinthu chinachake chikukonzekera kuchitika, anthu amatembenuza mitu yawo ndi kuchokapo; amaganiza kuti anthuwo ndi openga. Iwo akamuwona winawake akudzuka mu Mzimu ndi kunenera, kapena kupereka uthenga wochokera kwa Ambuye, bwanji, anthu a dziko la mpingo lero amaganiza kuti munthuyo wasokonezeka maganizo. Izo ndi zachirendo kwa iwo, chifukwa iwo ali pafupifupi chikhalidwe chomwecho, lero, monga Samariya anali mu tsiku limenelo.

⁸⁷ Koma, kumbukirani, pamene mafuko afika, kapena mpingo wa Mulungu nthawizonse ukafika mu chikhalidwe chimenecho, Mulungu amakhala wokhoza kudzutsa mneneri ndi Mawu a Ambuye kwa iwo. Ndithudi.

⁸⁸ Iwo anali ataiwala zimenezo, kalekale. Koma iwo ankayenera kukumbukira, mosalabadira kuti iwo akanakhoza kuyang'ana mmabuku awo, ndi kuwona ngati iwo anali ndi munthu wochokera ku ena a masukulu awo, dzina lake Dr. Amosi, kapena ayi. Iwo ankayenera kudziwa, kuti, "Mulungu wa Abrahamu anali wokhoza mwa miyala iyi kudzutsa ana, kapena aneneri, kuti abweretse Mawu Ake."

⁸⁹ Ndipo Mulungu yemweyo ndi wokhoza basi usikuuno monga Iye anali nthawi imeneyo. Ndipo iko kukanakhala, ndithudi, kunali kusamvetsetsa kwa anthuwo. Iye akhoza kudzutsa anthu, kudzoza anthu, kuti abweretse Mawu Ake. Iye akhoza kuyika Mawu mwa munthu, kumutumiza iye, ndi kukatsimikizira kuti Iye ndi Mulungu, kudzera mwa munthu ameneyo amene angadzichepetse yekha ndi kudzipereka yekha kwa Mulungu,

ndipo osawopa kumutenga Mulungu pa Mawu Ake. Iye ndi wokhoza kuchita zimenezo, ndipo Iye adzachita zimenezo. Iye analonjeza kuti Iye akanadzatero.

⁹⁰ Ndipo Mawu Ake, ndithudi, anatsimikiziridwa kwa iwo mu tsiku limenelo. Chifukwa, pamene kam'badwo komweko kanali mu kukhalapo, zonse zimene Amosi analosera zinakwaniritsidwa.

⁹¹ Ine ndikudabwa lero, tsopano, kuti ngati Amosi angabwere kwa ife, kodi ife tikanamulandira iye lero? Kodi Phoenix akanamulandira Amosi? Ngati kwinakwake kutsidya kwa phiri kuno, kwinakwake, kapena kumusi kuchokera ku gawo lina la dziko, kukanabwera munthu wamng'ono, wovala sanza monga choncho, kudzayenda kuno ndi kudzawaitanira atumiki ku dongosolo, ndi kuti, "Ine ndiri ndi Mawu a Ambuye," kodi mukuganiza kuti tikanamulandira iye? Ndithudi ayi.

Chinthu choyambirira chimene tikanamufunsa iye, "Kodi iwe uli ndi gulu lanji?"

⁹² Nanga bwanji ngati iye akanatembenuka, nkuti, "Gulu la Mmwambamwamba?" Izo zikanakhala ngati zachirendo kwa ife, ine ndikuwopa.

⁹³ Koma umo ndi momwe zinaliri mmbuyomo. Ndipo izo mwinamwake zingakhale chimodzimidzi lero ngati Amosi angabwere powonekera.

⁹⁴ Tiyeni, basi chifukwa cha zomwe ndanena, timutengere iye kuno, mphindi pang'ono chabe, ndi kuwona chimene ife tikuganiza kuti akanachita. Inu mukudziwa chimene iye akanachita? Ine ndikukhulupirira kuti iye akanatsutsana ndi dongosolo lathu lonse. Inde, bwana. Iye akanatsutsana ndi ziphunzitso zathu zachipembedzo. Iye akanawatsutsa Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, Achilutera, Akatolika, ndi Achipentekoste. Iye akanalowetsamo chinthu chonsecho mkati. Iye ndithudi akanadzatero. Iye akanadzatsutsana ndi ziphunzitso zawo zachipembedzo. Iye akanapita molunjika ku maziko achikhazikitso a Mawu, ndi kuyambira pa Mawu pomwe. Iye akanadzayambira msonkhano wake wokopa anthu pa PAKUTI ATERO AMBUYE.

⁹⁵ Bwanji, bwanji, inu mukuganiza kuti Phoenix ikanamulandira iye? Kodi inu mukuganiza kuti Louisville ikanamulandira iye; New York, Boston, Massachusetts, kapena kulikonse kumene kungakhale, California? Ayi, bwana. Iwo akanamutengera mnyamata wamng'onoyo mu ndende mwamsanga momwe iwo akanati amufikitse iye kumeneko. Ndithudi akanadzatero. Iwo ndithudi akanadzachita zimenezo. Ngati iye akanabwerera ku Mawu, ine ndikutsimikiza iwo akanatero, chifukwa gulu lililonse likanatsutsana naye iye. Sipakanakhala mmodzi wogwirizana naye, chifukwa iwo

akuyenera kuti agwiritsitse ku miyambo yawo kuti atsutsane ndi Mawu.

⁹⁶ Ife tikanayenera kukumbukira kuti iye ndi mneneri woona. Ngati iye anali, ndipo ngati iye anali mneneri wotumidwa kuchokera kwa Mulungu, iye akanadzakhala chomuzindikiritsa chimodzi kwa iye, chomuzindikiritsa chimodzi chotsimikizika choti ife tidziwe kuti iye ndi mneneri: iye akanadzakhala ndi Mawu. Chifukwa, ndiko kumene Mawu a Mulungu amabwerako, kunali kwa aneneri.

⁹⁷ Inu mukudziwa chimene iye akanadzachita? Iye akanadzazazira ndi kutsutsa kam'badwo kano. Iye akanadzatsutsa mkazi aliyense wodula-tsitsi mdzikoli. Iye akanadzatsutsa mlaliki aliyense wachipembedzo. Iye ndithudi akanadzatero. Iye akanadzatsutsa wosuta ndudu aliyense, mkazi aliyense amene amavala akabudula kapena matharauza. Iye akanadzawang'ambira iwo pakati. Chifukwa chiyani? Izo ndi zotsutsana ndi Mawu. Kulondola ndendende.

⁹⁸ Inu mukuganiza kuti ife tikanadzamulandira iye? Ayi ndithu. Iwo sakanadzamulandira iye.

⁹⁹ Iye akanadzatsutsa makhalidwe oyipa a mpingo. Iye akanadzagwedeza chala chaching'ono chamakwinya chija pa nkhope ya alaliki amenewo ndi kuti, "Inu mukutanthauza kundiwuza ine kuti mumadzitcha nokha mtumiki wodzozedwa wa Mulungu, ndipo nkuyima pa guwa ndi kuwalola akazi anu azivala mwachigololo pakati pa amuna anu, ndi zinthu monga choncho? Kuwalola atsikana anu azikula monga choncho? Inu mukuwalola amuna anu kukwatira kawiri kapena katatu, ndi kukhala madikoni mmipingo? Inu mukutanthauza kundiwuza ine kuti inu mukugwiritsitsa ku chiyeneretso chimene muli nacho mdzanja lanu, ndi kuwakana Mawu a Mulungu?" Oh, mai! Iye akanadzachizazira chinthucho. Inde, bwana. Chivundi cha mpingo, ndi chivundi cha mamembala, iye angadzazazire zimenezo. Mai! Membala aliyense, iye akanadzamukhadzulira pansu. Chiphunzitsa chirichonse chaku seminara chopangidwa ndi munthu, iye akanadzaching'amba chinthucho mzydutsa.

¹⁰⁰ Tsopano, kodi inu mungamulandire munthu wonga ameneyo? Ayi. Iwo sakanadzachita zimenezo. Iwo ndithudi sakanadzachita zimenezo. Iwo akanamutulutsa munthu ameneyo mu mzinda mwaliwiro momwe iwo akadathera. Bwanji, bungwelo bwenzi likukumana pamodzi, ndikuti, "Titi, ife tikuyenera kuchita chinachake chokhudza izi. Muwawuze osonkhana anu kuti asapite kumeneko kuti azikamva zimenezo." Ayi. Ayi. Iye sitingamulandire iye, ayi mwanjira iliyonse, ife sitikanadzamulandira iye. Ndithudi. Iwo sakanadzachita zimenezo.

¹⁰¹ Kumumvetsera iye akuzazira. Oh, ine ndikuzikonda izo apa. Ine ndikuyang'ana apo pomwe pa zimene iye ananena.

Iye anati, “Mulungu yemweyo amene inu mumadzinenera kuti mumamutumikira adzakuwonongani inu.”

¹⁰² Iye angadzanene chinthu chomwecho lero. Ife Achimereka tadzikulunga tokha mu zinthu zotengeka zochuluka, nyumba zazikulu zochuluka, ndi manambala aakulu mmabungwe athu, ndi kutchuka kwabwino konseku, ndi atumiki aku seminare amene anaphunzitsidwa kuti azikhala chete ndipo osanena kanthu za izo, chifukwa iwo akuwopa kuti iwo angachotsedwe mu mpingo. Ndithudi. Iye akanadzachizazira chinthu chimenecho mzidutswa, chifukwa izo zikutsutsana ndi Mawu. Ndithudi akanadzatero. Ndipo Mulungu yemweyo amene ife timanena kuti tikumtumikira adza—adzachiwotcha chinthu ichi, limodzi la masiku awa. Iye adzachiphulitsa icho mzidutswa.

¹⁰³ Amosi sakanadzasintha mawu ake, ngati iye akanadzakhala pano lero. Khalani mmbuyo momwe ku Mawu! Oh! Chiyani? Mvetsereni iye akuwauza iwo kumeneko, “Mulungu anakukondani inu. Iye anakubweretsani inu. Iye anakupangani inu kukhala anthu osankhidwa.”

¹⁰⁴ Ine ndikufuna kuti ndidzamumve iye mu mpingo wa Chipentekoste nthawi yina. Inu mukukhulupirira kuti iye ndi Amosi, mwina mwake iye angachoke pa nsana wanga, kwa kanthawi. Mukuona? Inde, iye akadadzawauza iwo. Iye sakanadzabweza nkhonya. Iye akanadzachiphulitsa icho mwamphamvu basi monga iye akadathera, ndi kuwawuza iwo pamene iwo anaperewera pa Mawu.

¹⁰⁵ Mulungu amene anakutulutsani inu mu zosungira mitembo zopangidwa-pakhomo izi, zopangidwa ndi anthu, zaka zapitazo! Zaka fifite zapitazo, abambo anu ndi amayi anatuluka mu kachitidwe kameneka kamene kanalimanga ndi kulitengera dziko mwa iwo. Ndipo Mulungu anatumiza chifundo Chake pansu ndipo anakuitanani inu mutuluke, kutalikana ndi tchimo ndi zinthu zimene—zimene zinali mu mpingo. Ndipo tsopano inu mwatembenuka, monga Samaria anachitira. Kuti, Mulungu anawatulutsa iwo kuchoka ku mayiko amenewo, ndipo iwo anatembenuka ndipo iwo anapanga mgwirizano ndi dziko limenelo, momwe ife tiriri lero, ndi kuyesera kupikisana ndi mipingo yayikulu yachipembedzo imeneyo. Ife tikumanga masukulu aakulu. Chiyani? Ife sitikusowa masukulu aakulu. Izo nzabwino; ine ndiribe chonena chotsutsa izo.

¹⁰⁶ Koma nthawi iliyonse imene inu mutenga woyambitsa kapena mtsogoleri amene amapita mu tsiku lake, chabwino, iye amachita bwino mu tsiku lake, koma, mwamsanga pamene iye wapita, ndiye iwo amamanga bungwe pamwamba pa ntchito yake. Ndiye iwo amabweretsa gulu la ma Rickys aang’ono mmenemo, ndi a Elvises, ndipo, chinthu choyamba inu mukudziwa, iwo amachipotoza chinthucho kuti chiwakomere

eniakewo. Ndipo kenako *wina* uyu amabwerapo ndipo amadzalowetsapo chinachakenso, chifukwa iye ndi wophunzira wamkulu waluntha wochokera ku Harvard kwinakwake, kapena chinachake. Ndipo chinthu choyamba, iwo amayamba kubailamo *ichi*, ndi kuchotsamo *Ichi*, ndi kunena kuti *Ichi* sichinkatanthauza *icho* ndi *icho*. Inu mwabwereranso mu chikhalidwe chakale chomwecho. Inde.

¹⁰⁷ Ngati Amosi akanakhala pano, iye akanachizazira chinthucho molunjika mpaka pansi. Iye samamanga konse msonkhano wake wokopa anthu pa kuchuluka kwa mipingo imene ikanayanjana naye iye. Iye sakanamanga konse mpingo wake pa bungwe linalake kapena magawo ena a mpatuko wa mpingo. Chinthu chimene iye akanachita, chikanakhala kumanga msonkhano wake wokopa anthu pa PAKUTI ATERO AMBUYE. Mulungu akanamuthandizira iye monga Iye amachitira nthawizonse, kutsimikizira kuti izo nzoona. Iye anati, “Muli vuto. Muli chipwirikiti mu mpingo wanuwo.”

¹⁰⁸ Kodi iye anganene chiyani lero? Kodi iye anganene chiyani ndi Mawu a Mulungu amenewo amene akuzendera kuno patsogolo pathu? Timoteo Wachiwiri 3, pamene Iwo anati, “Iwo akanadzakhala ammutu, odzikuza, okonda zosangalatsa koposa kukonda Mulungu; ophwanya malamalo, onenera zonama, osadziletsa, ndi onyoza iwo amene akuyesera kukhala olungama; okhala nawo mawonekedwe aumulungu, koma kukana mphamvu yake.” Inu mukuganiza kuti mneneri angawuke powonekera ndi kulambalala uneneri umenewo?

¹⁰⁹ Iye adzati, “Iwo wakwaniritsidwa pamaso panu lero,” momwe mpingo ukanati udzakhale wofunda, ndi momwe zinthu zimene iwo akanati adzachite. Iye akanadza—iye akanadzakukumbutsani Mawu a Mulungu amenewo. Iye akanadzakukumbutsani zimene Mulungu anati Iye akanadzachita mu tsiku lino, ngati Amosi akanawuka powonekera. Osati zokhazo, koma Mulungu akanadzatsimikizira, mwa Amosi, chimene Iye analonjeza kuti adzachita mu tsiku lino. Ndithudi. Iye akanadzatero. Iye anachita izo mu tsiku limenelo. Iye wakhala akuchita izo nthawizonse. Ndithudi.

Ife sitikanadzamulandira Amosi ngati iye akanadzuka powonekera.

¹¹⁰ Tsopano, motani, “Mawonekedwe aumulungu amenewo,” kuyima pamenepo mu—mmakwaya, ndi—ndi pozungulira, makwaya a mwinjiro wawutali, ndi—ndi kumayimba ngati Angelo; ndi kumavina, usiku wotsatira, ngati ziwanda. Uko nkulondola. Mukuona? Ndizo ndendende choonadi. Ena amatuluka atavala miinjiro yayikulu, yayitali, yowoneka—mwamaluwa maluwa monga choncho, ndi kumawoneka ngati mtundu *wina* wa Chinthu cha ungelu; ndi kuimirira pamenepo

ndi kukana Mawu, monga mzimu woyipa uliwonse ukanachitira. “Kukhala nawo mawonekedwe aumulungu, koma nkumakana mphamvu yake.” Kupita, kumakayankhula za ubatizo wa Mzimu Woyera, iwo, bwanji, iye anga—iye angakuthamangitseni kukuchotsani mu tchalitchi. Mukuona? Chifukwa chiyani? Iye akuyenera kuteru. Koma iwo amayima mmipingo iyi ndi kuwalola mamembala awo, mu chipinda chapansi, kumapanga kuzithyola ndi gwedemula.

¹¹¹ Ndipo athu otchedwa ma Y.M.C.A., ine ndikudabwa chimene C ameneyo amayimira. Kuyenda mwa iwo, iwe sungamve kanthu koma Dzina la Ambuye u- . . . Kodi limenelo ndi Gulu la Achinyamata Otukwana?

¹¹² Ine ndinakhala, osati kale kwambiri, mu hotelo, inali kutsidya la Y.W.C.A. Ndipo icho chinali chamanyazi kuwawona atsikana aang’ono amenewo kunja uko ali pansi, mpaka pafupifupi naini koloko, akuyesetsa kuthyola miyendo yawo, akuchita kuzithyolako. Uko nkulondola. Ndipo onse a iwo, mamembala a mpingo, amayimba mu makwaya, ndi kuphunzitsa Sande sukulu. Sikanthu koma mdierekezi, kuwaphunzitsa ana aang’onowo kunja uko pansi, kachitidwe kamene kapangidwa, kotchedwa chipembedzo. Ndithudi. Mneneri woona angachizazire chinthu chimenecho kuchibwezera ku utsi wa gehena kumene icho chinachokerako. Ndithudi ndi zoon.

¹¹³ Inu mukuganiza Amosi angayime pa nsanja ndi kulalikira Uthenga, ndi kuyang’ana uko pa gulu la akazi odula tsitsi ndipo osadzudzula izo? Inu mukuganiza kuti iye sangabwereze kuwerenga Yesaya 5, ndi Akorinto Woyamba 14? Ndipo, oh, kodi iye—kodi iye sangatsanulirepo zimenezo? Ndithudi. Iye angatero. Kuyenda mmisewu ndi kuwawona akazi atavala zovala zazing’ono izi, kumawoneka ngati amuna, zothina kwambiri mpaka khungu kukhala kunja, pafupifupi; akutsika mmusi, akuzipotokola, kumazithyola, kumayenda monga choncho, kumapanga okha phokoso akamayenda, ndipo inu mukuganiza kuti munthu wa Mulungu sangayime pa guwa ndi kuchizazira chinthu chimenecho? Pamene, izo sizimalankhulidwa kawirikawiri kuchokera pa—pa guwa. Ndipo umo ndi mmipingo ya Chipentekoste, nayonso. Ndizo kulondola ndendende. Sizikadapanga kusiyana kulikonse kwa Amosi. Uh-huh. Ena. . . Iye angakhale mmodzi amene anganene zimenezo. Iye sangachite mantha, chifukwa ndi wodzozedwa wa Ambuye. Ndipo ngati iye anali ndi PAKUTI ATERO AMBUYE, ankayenera kukhala Mawu a Ambuye.

¹¹⁴ Iye anabwera ku Samaria, osati kuti adzayang’ane pa kukongola kwawo, kuti adzawerenge kuchuluka kwa mabungwe, ndi manambala angati amene iwo anali nawo.

¹¹⁵ Monga ine ndinanena usiku wina, zikuwoneka kuti ziri,

lero, kuti mpingo wonse wamangidwa pa, chinthu chachikulu pakati pa abale lero, cha mipingo, ndi, “chiwerengero, chiwerengero,” mmodzi akuyesetsa kumuposa mzake winayo. “Chiwerengero!” Mulungu samawerenga chiwerengero. Iye amawerenga khalidwe. Khalidwe ndi limene Mulungu akufuna kuti alipeze, winawake amene Iye angayikepo manja Ake, winawake amene angayime motalika kokwanira.

¹¹⁶ Monga ife tinanenera, “Zigamulo! Chaka chonse, takhalapo ndi zigamulo *zochulukwa*.” Ndizo *miyala*, “zovomereza.” Ndipo mwala ndi waubwino wanji ngati palibe mmisiri wokhala ndi Mawu akuthwa a Mulungu, kuti amudule iye kukhala mwana wa Mulungu, kapena mwana wamkazi wa Mulungu, ndi kumuyika iye mu Mpingo umene uli wake? Miyala yogudubuzika siingamange nyumba. Inu muyenera kuidula iyo ndi kuyisongola iyo.

¹¹⁷ Ife tikusowa amuna lero, amuna odzozedwa, monga Amosi anali, amene angalidulire dziko kulichotsa kwa mkazi ameneyo ndi kumupanga iye mwana wamkazi wa Mulungu, kulidula dziko limenelo kulichotsa kwa munthuyo. Mosalabadira kuti ndi matrasti angati amene anamutayira iye kunjira, kapena china chirichonse, iye angaime pa PAKUTI ATERO AMBUYE. Inde.

¹¹⁸ Ife sitingamulandire Amosi, ine sindikuganiza, monga chonchi. Kodi inu mukuganiza kuti Amosi akanadzachita chiyani iye akanalowa mu mpingo wa Pentekoste wa lero, umadzinenera kuti umatsogozedwa ndi Mzimu Woyera, ndipo kenako nkuwona chinthu chomwecho mu mpingo wa Chipentekoste umene umadzinenera kuti umatsogozedwa ndi Mzimu Woyera? Ine ndikudabwa. Tsopano, ife tikhoza kuyankhula za Abaptisti, ndi Amethodisti, ndi Achilutera, koma, pamene zifika pa khomo lathu lomwe lodetsedwa, ndiye nanga bwanji zimenezo? Achoka ku Mawu a Mulungu! Chinachake chinalakwika, penapake. Ndiko kulondola ndendende. Eya. Iwo amabwera ndi kudzachita zinthu zosiyanasiyana zonsezi, ndi kumadzinenera kuti akutsogozedwa ndi Mzimu, kuvina mu Mzimu, nthawizina ngakhale kuyankhula mmalirime.

¹¹⁹ Ine ndimakhulupirira mu kuyankhula ndi malirime. Ine ndimakhulupirira mu kuvina mu Mzimu. Ine ndimakhulupirira mu kufuula. Koma pali zambiri zimene zimayenda ndi izo. Uko nkulondola. Inu mumachita zinthu zonsezo, ndipo nkuwakana Mawu, ndiye kuti pali chinachake cholakwika penapake, muli ndi mzimu wolakwika. Uh-huh. Mulungu samawatsogolera anthu Ake ku zinthu zoterozo, mulimonse. Ayi. Iye samatero.

¹²⁰ Ine ndikuganiza kuti yafika nthawi basi pafupifupi phwando lina lotuluka, Phwando lina la Tiya laku Boston, momwe tinganenerere. Mpingo ukusowa chimodzi. Iwo ukusowa kutsukidwa kwabwino kwenikweni.

¹²¹ Pamene, Joan waku Arc, mmasiku apitawo, mpingo wa Katolika unaphonya kudziwa kuti iye anali woyera pamene iye anali moyo, chifukwa iye ankawona masomphenya, ankatha kutanthauzira maloto, mkazi wodzazidwa ndi Mzimu. Ndipo Mulungu anamugwiritsa ntchito dona wamng'onoyo. Ndipo iwo ankaganiza kuti iye anali mfiti. Ndipo iwo anamuwotcha iye pa nkhuhi, ngati mfiti. Inu mukudziwa zimenezo. Ansembe Achikatolika anachita zimenezo iwoeni. Zaka mahandirede zinadutsa, ndipo iwo anadzapeza kuti iye anali woyera. Kenako, pamene iwo ankati amupange iye kukhala woyera, iwo ankayenera kuti alape. Chotero iwo anawafukula matupi a ansembe amenewo ndi kuwaponyera iwo mu mtsinje, kuti alape. Inu mwawona, izo zinadutsa pamenepo ndipo iwo analephera kuti awone izo. Iwo anachita pafupifupi chinthu chomwecho ndi Patrick Woyera ndi ena onse a iwo.

¹²² Nzosadabwitsa Yesu anati, “Mumakongoletsa ndi kuyetsa manda a aneneri, ndipo inu ndi amene munawayika iwo mmenemo.” Izo nzoona. Chimene ife tikusowa lero ndi Amosi amene ati adzabweretsenso Mawu a Ambuye kwa ife. Ndithudi amatero.

¹²³ Tsopano, zodzinenera zathu ndi zinthu sizitanthauza kalikonse pokhapokha ngati Mzimu wa Mulungu utakhala pamenepo kuti uyikire kumbuyo zodzinenera zathu. Ngati miyoyo yathu sikufanana ndi zodzinenera zathu, ndiye kuti pali chinachake cholakwika.

¹²⁴ Joan waku Arc anatsogolera France ku kusintha. Iwo ankasowekera kusintha. Ndizo ndendende zimene iwo anachita. Iwo ankasowa kusintha, ndipo iye anatsogolera iko. Koma kutachitika kusinthako, pamene anapangira kulakwitsa, iwo ankasowekera kusintha-motsutsa kuti awongole—kuti awongole chimene iwo ankachisinthacho.

¹²⁵ Ine ndikuti mpingo wa Chipentekoste ndi chinthu chapafupi kwambiri chimene ndikuchidziwa kwa Baibulo lero. Ngati sunali iwowo, ine ndikanakhala mwa wina. Izo nzoona. Ine sibwenzi ndikuima pano ndi kumataya nthawi yanga, kuyankhula kwa anthu Achipentekoste, ngati zikanakhala kuti sindikuganiza kuti zinalipo ziyembekezo. Kulondola. Pentekoste ndi yolondola. Koma pamene tisowa Pentekoste kuti isonkhane pamodzi ndi kudzaswa miyambo yathu, zikatero ife tikusowa kusintha-motsutsa. Ife tikusowa kubwera-motsutsa; ine ndiri...osati kudzinenera kwa Chipentekoste, koma kubwera koyera kwa Chipentekoste.

¹²⁶ Mulungu ndi woyera. Iwo amene amakhala moyo mwa Iye akuyenera kukhala moyo woyera. Iye ndi Mulungu woyera. Baibulo linati, “Popanda chiyero, palibe munthu amene adzamuwone Ambuye.” Izo nzoona. Moyo Wake ndi woyera. Ndipo ngati Moyo Wake uli mwa inu, umakupangani inu

kukhala woyera. Popanda iwo, inu simudzawawona Ambuye. Ndipo onani kumene iye akugwerako.

¹²⁷ Ife ndife chinachake monga Israeli anali mmasiku amenewo, mulimonse. Israeli ankaganiza, chifukwa iwo anali kulemera, chirichonse chinkayenda mwabwino bwino. Iwo anali ndi mgwirizano, mmasiku awo, ndi mizinda ina. Ndipo iwo anali ndi mgwirizano. Boma linali ndi mgwirizano ndi atumiki, ndi ansembe, ndi aneneri. Ndipo iwo ankaganiza kuti izi zinali zabwino. Ndipo iwo ankaganiza kuti izo zinali zowakondweretsa Ambuye. Koma iwo anali ndi munthu wamng'ono amene anawuka ndi kuwabweretsanso iwo mmbuyo kachiwiri. Uko nkulondola.

¹²⁸ Chifukwa chakuti iwo analemera, pamenepo ndi pamene ife timalakwitsira. Kulemera si chizindikiro cha mdalitso wauzimu. Uko nkulondola. Ayi ndithu sindizo. Kulemera, nthawizina, ndi cholepheretsa.

¹²⁹ Inu mukukumbukira zimene Ambuye ananena za Israeli? “Pamene iwe unali wamng'ono, pamene iwe unalibe kanthu, pamene iwe unakagona mmagazi ako omwe mmunda, panalibe aliyense woti akuyeretse iwe, Ine ndinakutengera iwe mkati. Kenako iwe unakanditumikira Ine. Koma pamene iwe unadzakula mokwanira mpaka nkumaganiza kuti uli bwino ndi wodziteze wekha, ndiye iwe unandisiya Ine.” Iwo amachita zimenezo nthawizonse.

¹³⁰ Uziya, monga ine ndinayankhulira pa kadzutsa wa Amuna Amalonda mmawa wina, iye anali munthu wopambana. Iye anagwiritsitsa kwa Ambuye. Koma tsiku lina Mulungu atatha kumulimbitsa iye. . . Ndipo iye anali chitsanzo chopambana kwa Yesaya mneneri. Koma atatha kukhala wamphamvu, ndipo nkumangika, mafuko anayamba kumuwoya iye. Iye anamanga makoma ake ndipo anayamba kupeza zinthu zokongola. Iye anayamba kudzikuza. Iye anayamba kuyang'ana momwe iye analiri wamkulu. Ndipo kenako iye anayesetsa kuti atenge malo a mlaliki. Ndipo Mulungu anamukantha iye ndi khate, ndipo iye anafa ali wakhate. Mukuona? Ife sitimafuna konse kuti tizifika podzikweza mmwamba, mmitima mwathu.

¹³¹ Ndipo nthawizina, pamene tiwona mabungwe athu akuchita bwino, timayamba kunena kuti, “Ndife gulu lalikulu. Ndife gulu lalikulu la Chipentekoste limene liripo. Ife tiri nawo ochuluka kuposa ena onsewo.” Kapena, “Simungapite Kumwamba pokhapokha inu mutakhala a gulu lathu,” kapena chinachake. Pamene inu mufika mwanjira imeneyo, inu mwadzilekanitsa nokha ku Mawu a Ambuye. Kulondola. Kumbukirani, bulangeti limakhala lalikulu ngati lingamufikire mbale wanu. Ndiko kulondola ndendende. Mulowetsenimo iye.

¹³² Oh, momwe ife tikusowekera, lero, kuyitana kubwerera ku Mawu a Ambuye. Penyani, lero. Ndipo fuko lathu likusowa

kuyitanidwanso kubwerera.

¹³³ Ndidzayankhula, limodzi la mausiku awa, ngati ndingathe, ine ndikufuna. . . Ndiri ndi chitsutso. Ine ndikuyenera kudikira mpaka ine nditawabweretsa alaliki onse pamodzi. Eya. Ine ndikufuna kudzawutsutsa m'badwo uno za Magazi a Yesu Khristu, ndi kutsimikizira izo kwa inu. Mukuona? Tsopano, ine ndikhoza, kupita kwinkwaka kuti ndikachite zimenezo. Koma tidzatero, ife tiwona ngati ife tingadzakhale ndi kadzutsa mmawa wina, ya atumiki okha. Ndipo ine—ine ndikufuna kudzatero, Ambuye akandithandiza ine, kudzawonetsera ndendende kumene ife tiri—kumene ife tikulowera, njira yolakwika. Ife tikuyenera kubwerera. Palibe njira ina koma kubwerera. Kulondola.

¹³⁴ Tayang'anani fuko lathu lero. Taonani zimene tikuyesetsa kuti tichite, chinthu chomwecho chimene chinachitika mu m'badwo wa mdima, kuyanjanitsa mpingo ndi dziko pamodzi.

¹³⁵ Tayang'anani pa mgwirizano, kulimikizana, kapena a—Bungwe la Mipingo ya Padziko. Mipingo yonse ikupita mu Bungwe la Mipingo ya Padziko ili, ndipo iwo amaganiza kuti uwu ndi umodzi wa Mulungu. Chifukwa, mipingo yonse, United Brethren, amuna a mipingo ya chikhazikitso, akupita mu bungwe limodzi lalikulu ili. Izo ndi chifukwa cha kusowa kudziwa Mawu a Mulungu. Mneneri anayankhula kuti chinthu chimenecho chidzachitika, “Iwo adzapanga fano kwa chirombo, ndipo icho chidzakhala ndi mphamvu yoyankhula.”

¹³⁶ Oh, kodi inu mukuganiza kuti Amosi akanayima pa guwa usikuuno kumusi kuno, ngati iye akanakhala ku Phoenix, ndipo nkulephera kufuula mokweza pa chinthu chimenecho? Sikuti akanakhala kuti akulimbana nafe, abale, koma akanakhala akutsutsana ndi kachitidwe kamene kakutikokera ife kutali ndi Mawu. Icho ndi chimene iye akanadzachita. “Kodi amuna amenewo angayende limodzi bwanji?” Baibulo linanena apa, umu, Amosi. Ambuye anati, “Awuze anthuwo, ‘Awiri angayende bwanji limodzi, pokhapokha ngati atagwirizana?’”

¹³⁷ Tsopano, ife tiwatenga bwanji magulu athu Achipentekoste ndi kukalowa mu Bungwe la Mipingo ya Mdziko, pamene theka la iwo mmenemo, oposa theka, eyite-faivi kapena nainte-faivi peresenti, akukana kubadwa kwa namwali? Iwo amakana. Ine ndikuganiza, nainte-naini peresenti a iwo amakana, iwo amakana machiritso Awuzimu. Iwo amakana mfundo za Baibulo. Iwo amakana kuyankhula ndi malirime. Gulu la Chipentekoste lokha limatenga zimenezo. Ndipo ife tingadzalumikize bwanji tokha ndi iwo mu umodzi? Zingatheke bwanji kuti tikhale amodzi ndi iwo? Ife tingayende bwanji ndi iwo popanda kugwirizana nawo iwo? Inu mungachite bwanji zimenezo? Inu mukuyenera kukana chikhulupiro chachikulu

cha uvangeli chimene muli nacho, mfundo zachikhazikitso za Baibulo, kuti muyende ndi iwo.

¹³⁸ Ine ndikukuuzani inu, Mulungu amamuitana munthu payekha. Iye akukuitanani inu, ngati munthu panokha, kuti muzikhala ndi Mawu Ake ndi kukhala ndi Iye.

¹³⁹ Zingatheke bwanji kuti Mulungu aziyenda ndi iwo, pamene tizikhulupiriro tawo tomwe, topangidwa ndi nzeru zawo zachidziko, tikumakana Mawu Ake? Pamene kachikhulupiriro kavomereza chiphunzitso cha gulu la anthu, pamodzi, ndi kuwakana Mawu kukhala otero, ndiye inu mwamuchotsa Mulungu kwa inu. Mulungu ndi woyera. Ndipo Mulungu, Baibulo limati, Iye amawayang'anira Mawu Ake, kuti awatsimikizire Iwo. Ndipo Iye angawatsimikizire bwanji Mawu, pamene Mawuwo palibepo pamenepo? Ndi chifukwa chake tiri ndi mamembala mmalo mwa ana. Ndizo, tiri ndi kachikhulupiriro. Ndipo aliyense akhoza . . .

¹⁴⁰ Dziko likufunafuna munthu wapamwamba. Iwo akugwirira ntchito . . . Iwo akufunafuna chinachake chimene chingawalole iwo kugwiritsitsa ku kuvomereza kwawo kwa Chikristu ndi kumakhala mulimonse mmene iwo akufunira. Akazi amafuna kuti azichita monga Hollywood ndipo nkumadzinenerabe kuti iwo ali nawo Mzimu Woyera. Alaliki akufuna azimanga tchalitchi chachikulu kwambiri ndi kumachita zinthu zonsezi, ndi kukhala ndi madikoni amene anakwatirapo nthawi zambiri. Ndipo—ndipo nkumakhoza kuchita zinthu zazing'ono izi ndi kumavala zovala *izi*, iwo amadzitcha izo kumasulidwa kwa akazi.

¹⁴¹ Kodi mukuganiza kuti Amosi angayime nazo chete zimenezo? Ayi. Ndithudi iye sangatero. Inu mukuganiza kuti Amosi angakhale chete, ndi kukumana ndi a mawudindo ndi mabishopu kumeneko, ndi kuti, “Abale, ndikuganiza kuti inu mwachita chinthu chachikulu.”

¹⁴² Iye angati, “Inu gulu la zigawenga! Onyenga inu! Inu okana Chikhulupiriro!” Iye anganene chinthu chomwecho chimene Mikaya ananena, tsiku lija pamaso pa aneneri foro handireded Achiheberi odzipanga okha awo.

¹⁴³ Iwo anati, “Mu chiwerengero, unyinjira muli, ndipo mumakhala chitetezero.” Zimatengera pamene inu mukufuna kugwiritsa ntchito Lemba limenelo.

¹⁴⁴ Ine ndikhoza kunena kuti, “Yudasi anapita ndipo anakadzinyonga yekha; ndipo inu mupite mukachite chinthu chomwecho.” Izo sizikugwira ntchito pamenepo.

¹⁴⁵ Ndipo sizikugwira ntchito, kuti, “Mu uphungu wochuluka muli chitetezo.” Mpingo wa Katolika ndiye kuti uli nacho icho pa inu nonse.

¹⁴⁶ Mu Mawu a Mulungu ndi mmene muli chitetezero. Baibulo linati, “Dzina la Ambuye ndi nsanja yamphamvu. Olungama amathamangiramo ndipo amatetezeka.” Ndipo ndi malo okhawo otetezeka amene ndikuwadziwa. Aneneri nthawizonse ankakhulupirira zimenezo. Pamene Abrahamu anafa, pamene. . . Pamene Yobu anafa, iye anadziyika yekha mu dziko lolonjezedwa, manda ake.

¹⁴⁷ Pamene Abrahamu anafa, iye anagula gawo la malo pafupi ndi malo omwewo, pafupi ndi Yobu. Kodi iye anachita chiyani? Iye ankamuyang’ana mneneri ameneyo. Iye ankadziwa kuti ameneyo anali munthu wa Mulungu, ndipo iye anati, “Ine ndikudziwa Muwomboli wanga ali moyo, ndipo pa masiku otsiriza Iye adzaima pa dziko lapansi. Ngakhale mphutsi za khungu zitawononga thupi ili, komabe mu thupi langa ine ndidzamuwona Mulungu.” Eya. Ndipo Abrahamu ankadziwa zimenezo. Iye anamuyika Sarah kumeneko. Iye anagula gawo la malo, ndipo anakamuyika. . . Iye, mwiniwake, anakayikidwa kumeneko.

¹⁴⁸ Isaki, pamene anafa, iye anatengedwera kumeneko ndipo anakayikidwa kumeneko. Isaki anabala Yakobo.

¹⁴⁹ Ndipo Yakobo anafera uko mu Igupto. Koma iye asanamwalire, anamuyitana mwana wake mneneri, Yosefe. Ndipo iye ankadziwa kuti iye anali mneneri, munthu wauzimu, ankamasulira maloto, ndipo ankawona masomphenya, amakhala olondola mwangwiro nthawi iliyonse. Iye anati, “Bwera kuno, Yosefe, mwana wanga mneneri. Ika dzanja lako pa ntchafu iyi imene Mulungu wamphamvuzonse anandigwira ine zaka zapitazo, ndipo anasintho dzina langa kuchoka ku ‘wolanda’ kukhala ‘kalonga ndi Mulungu.’ Udzaike manja ako pamwamba apa ndipo ulumbire pa Mulungu ameneyo kuti iwe sudzandiyika ine kuno mu Igupto.” Chifukwa chiyani? Chifukwa chiyani? Kodi izo zinapanga kusiyana kotani?

¹⁵⁰ Ndi zomwe iwo amanena lero, “Izo zinapanga kusiyana kotani?” Iye timatenga gulu la anthu, timawatenga iwo kuti ajowine mpingo, ndi kuchoka mmisewu. Inu nthawizina mumamupanga iye kukhala mwana wapawiri wa gehena kuposa momwe iye anali kunja uko pa msewu. Uko nkulondola. Zimapanga kusiyana.

¹⁵¹ Yosefe, pamene iye anafa, iye anayankhula, anati, “Tsiku lina Ambuye Mulungu adzakuchezerani inu.” Iye anali mneneri. Iye anati, “Ambuye Mulungu adzakuchezerani inu. Ndipo inu musadzasiye mafupa anga kuno, koma mudzawatengere iwo kumtunda uko mdziko lolonjezedwa.” Chifukwa chiyani? Iye ankadziwa kuti Chipatso choyambirira cha chiwukitsiro chidzachokera ku dziko lolonjezedwa. Ndizo ndendende.

¹⁵² Yesu, pamene Iye anafa, ndipo anawuka mmawa wa Isitala, Baibulo linanena, kuti, “Oyera ambiri amene anagona mu fumbi

anawuka, ndipo anatuluka mmanda ndipo anawonekera kwa ambiri.” Anali ndani uyo? Abrahamu, Isaki, Yakobo, Yosefe. Chifukwa chiyani? Iwo anali pamalo oyenera.

¹⁵³ Ndi chifukwa chake ine ndimanena kuti izo zimapanga kusiyana. Inu musangondiyika ine kunja kuno mu Methodisti, Baptisti, kapena mpingo wina. Mudzandiyike ine mwa Yesu, “Pakuti iwo amene ali mwa Khristu Mulungu adzawabweretsa limodzi ndi Iye pamene Iye azidzabwera.” Ndipo izo zimapanga kusiyana. Ndithudi, izo zimatero.

Musalole wina akuwuzeni inu, “Chifukwa mwajowina tchalitchi.”

¹⁵⁴ Amosi sakanangokhala chete chifukwa cha zimenezo. Iye akanati, “Mulungu yemweyo amene inu mukunena kuti mukumutumikira. . .”

¹⁵⁵ Ine ndinganene ichi mu Dzina la Ambuye: Mulungu yemweyo amene fuko ili likuyenera kumuyimira adzaliwononga fuko lino. Iye adzaiwononga mipingo iyi. Mulungu wa Kumwamba adzatsitsira pansu mkwiyo Wake mu chiweruzo ndi kuiwononga mipingo iyi, yotchedwa mipingo. Mukumbukire, kutenga mawu anga.

¹⁵⁶ Palibe aliyense amene angajowine Mpingo. Inu mumajowina loji. Inu simumajowina Mpingo. Inu mumabadwira mu Mpingo. Mukuona? Inu mumajowina loji ya Methodisti, loji ya Baptisti, loji ya Katolika, loji ya Pentekoste. Koma inu mumabadwira mu Mpingo wa Mulungu wamoyo; ndipo icho ndi chimene Iye akudzera, Mpingo umenewo. Chotero, ife tiri nawo malozi, osati Mpingo. Chirichonse chikhoza kusunkhana mu loji imeneyo, achinyengo ndi china chirichonse. Koma ine ndikudziwitsani inu izi pakali pano, molingana ndi Mawu, simumakhala wachinyengo mmodzi mu Mpingo wa Mulungu wamoyo. Simumakhala kalikonse Mmenemo koma oyera.

¹⁵⁷ Tsopano, umembala ukhoza kukutengerani inu mkati. Ndipo inu mukuganiza—mukuganiza kuti Amosi sakanazizazira zimenezo? Iye akanachigwedeza chinthu chimenecho mpaka ku maziko ake. Iye ndithudi akanatero.

¹⁵⁸ Taonani. Pamene Israeli anali pa ulendo wake, akupita ku dziko lolonjzedwa, motsogozedwa ndi Mzimu Woyera, Lawi la Moto linali patsogolo pawo, Thanthwe lokanthidwa linkawatsatira iwo.

¹⁵⁹ Ndipo pamenepo panadzatulukira Moabu, amene anali mchimwene. Kumbukirani, iye anali gawo la Israeli, nayenso. Iye anali gawo, monga wochokera ku fuko la Chiyuda limenelo, chifukwa anali mwana wa Loti mwa mwana wake wamkazi. Izo zinatulutsa Moabu.

¹⁶⁰ Ndipo tayang’anani pa Balamu, wansembe, anabwera kumeneko ndipo anadzapanga guwa, anadzapereka nsembe

za mtundu womwewo, wachikhazikitso basi monga iye akanakhalira. Mukuona? Ndipo iye anali nawo otchuka. Iye anali ndi mfumu. Iye anali ndi amuna onse aakulu, akalonga ndi adindo, atayima naye.

¹⁶¹ Koma panali Mmodzi amene anaima ndi Mose amene iye sankamuwona. Ameneyo ndi Amene anayima ndi Amosi. Ameneyo ndi Amene ati adzayime ndi munthu aliyense amene ali pano, usikuuno, amene adzaima ndi Mulungu ndi chirungamo. Ziribe kanthu ndi amphamvu ochuluka bwanji, mafumu amene ali kumeneko, ziribe chinthu chimodzi chochita ndi zimenezo. Iwo sadzakwanitsa konse kutemberera chimene Mulungu wachidalitsa. Chifukwa chiyani? Iyo ndi Mbewu yamoyo. Ndi Mawu a Mulungu. Iyo idzakula mpaka ku ungwiro Wake. Oh, zizindikiro za Mulungu wamoyo mu msasa! Ndizo, zinkawoneka ngati kuti Israeli anali atachita cholakwika kumusi kumeneko. Koma iwo analephera kuti awone Thanthwe lokanthidwa limenelo, ndi Chitetezero chimenecho chikupangidwira Israeli. Ndipo uko kunali mfuu wa Mfumu mu msaso. Mulungu anali ndi iwo. Chifukwa chiyani? Iye anali akuchiritsa odwala, ndi kumachita zozizwitsa zazikulu, ndi zizindikiro ndi zodabwitsa, ndipo Lawi la Moto litapachikika pa iwo. Mose anali akutsatira Lawi la Moto. Ana a Israeli anali akumutsatira Mose. Ndipo iwo anali pa ulendo wawo waku dziko lolonjezedwa, ndipo panalibe choti chiwaletse iwo. Amen.

¹⁶² Oh, kodi izo sizingabwerezedwe mophweka lero, ngati Mulungu angamtenge winawake mdzanja Lake, mu ulamuliro Wake? Lawi la Moto lija likanali lamoyo. Iye akanali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Mawu akanali moyo.

¹⁶³ Mulungu, titumizireni ife Amosi amene . . . amene adzaimire Choonadi ndi cholondola, adzagwedeze zinthu izi.

¹⁶⁴ Inu mukuti, “Kodi ife tikanakhoza . . . Kodi mukuganiza kuti iye angadzakhale ndi zotsatira za mtundu wanji?”

¹⁶⁵ Chabwino, iye angadzakhale ndi zotsatira, mpaka iye angadzawaitane onse amene Mulungu anali atawadzodzeratu kuti adzaitanidwe. Ndiwo amene iye akanadzawapeza. “Onse amene Atate andipatsa Ine adzabwera.” Inde.

¹⁶⁶ Mikaya anali pamaso pa Ahabu, ndipo Ahabu ankamuda iye. Gulu lonse la azitumiki linali likumutsutsa iye. Ndipo iwo onse anali atadzozedwa, nawonso, koma kudzoza kwawo sikunagwirizane ndi Mawu. Ine ndikuganiza, mwinamwake, Amosi anagunda chinthu chomwecho.

¹⁶⁷ Pamene ansembe anapita mu msewu, anati, “Tsopano, dikirani miniti. Kumene—kumene . . . Ndiwonetse ine zokuyenereza zako. Unachokera ku sukulu iti? Unachokera mu banja liti? Kodi ndiwe a . . . Anakupanga iwe kukhala wansembe ndi ndani?”

Iye akanati, “Mulungu anandipanga ine.”

“Ndiwe wochokera ku sukulu iti?”

168 “Yehova Mulungu. Ine ndiri ndi PAKUTI ATERO AMBUYE.” Iwo adzamumvera iye? Ayi ndithudi. Iwo sankafuna kumumvera munthu ameneyo. Ndithudi ayi. Iwo sanafune. . .

169 Ndipo, komabe, amuna amenewo mwina akanati, “Ndine wodzowedwa. Chabwino, ine ndi wa mpingo wawukulu wa Afarisi kuno. Taonani mmene Mulungu watidalitsira ife. Ife tinaikamo maguwa agolide. Tinayikapo akachisi. Ife tinachita zinthu zonsezi. Ndipo, oh, chopereka chathu cha umishonare ndi chachikulu kuposa mipingo ina yonse mu Yudeya yense. Chabwino, ife timachita zinthu zonsezi *pano*. Anthu athu ndi opereka chakhumi chochuluka, ndi zonsezo.” Komabe Mikaya kapena. . .

170 Amosi anayima pamenepo ndipo anati, “Mulungu amene inu mukudzinenera kuti mumamutumikira adzakuwonangani inu.” Ndipo izo zinachitika mwanjira imeneyo.

171 Tsopano, ine sindikutsutsa madongosolo a umishonare. Ine sindikutsutsa mipingo yayikulu. Koma, vuto lake ndi lakuti, anthu amayika maso awo pa zimenezo, ndi pa. . . kuchoka pa Mawu. Ndipo, potsiriza, izo zimakutengerani inu mu chinthu chimenecho, ndipo inu mumadzipeza nokha mukuterereka. Bwererani ku Mawu. Musati muchoke kwa Iwo. Oh, momwe ife tikusowekera kufuula, kuchokera mu chipululu lero. Ndithudi ndi zoon tsopano. Ndithudi.

172 Zifukwa zina, anthu amalingalira. Iwo amafuna kulingalira. Ndicho chinthu choyamba chimene anachepeza. . . Icho ndi chimene chinataya chiyanjano cha mtundu wa anthu, ndi pamene Satana anayambitsa dongosolo la kulingalira motsutsa Mawu kukhala chomwecho. Ndipo zinkamveka zanzeru kwambiri.

173 Tiyeni tingomutenga Satana, chimene iye mwina anali atanena kwa Eva, pamene Mulungu anawamangira iwo linga mkati mwa Mawu Ake.

174 Ndicho chinthu chokhacho chimene Mulungu anawapatsapo anthu Ake kuti awalimbikitsire nacho iwo kwa mdani, chinali Mawu. Iye sanatipatse ife kachikhulupiriro. Iye sanatipatse ife kalikonse koma Mawu Ake. Ndizo zonse. Ndipo Mulungu ndi wopandamalire, wamphamvuzonse, wosasintha. Iye sangakhoze kusintha. Dongosolo Lake loyamba ndi langwiwo. Iye samasowa kuti azilisintha ilo.

175 Lingaliro Lake loyamba, pamene munthu anachimwa ndipo anawoloka phompho lalikulu lija pakati pa iye ndi Mulungu, osazisiyira yekha njira yobwererera, Mulungu, wodzaza chifundo ndi chisomo, anavomereza mlowammalo. Ndi Mulungu yekha amene ali wodzaza chifundo ndi chisomo angachite chinthu choterocho. Iye anavomereza mlowammalo, ndipo mlowammalo ameneyo anali magazi. Amenewo ndi malo

okhawo amene munthu angathe kubweranso mu chiyanjano ndi Mulungu, ndi pansu pa magari okhetsedwa. Ndipo sipanakhalepo nthawi iliyonse imene munthu akanayanjana kwa Mulungu, kokha mwa magari. Ndipo ndi zoonza kwambiri, pamene iye amayanjana ndi Mulungu.

¹⁷⁶ Tsopano, Eva analekelera zigwiriro. Eva anayamba kulingalira. Satana ananena monga chonchi, “Tsopano, ndiwe . . . Iwe sukudziwa. Iwe sunakhalebe ndi kuphunzitsidwa kulikonse. Ndine purofesa wa seminare kunjika kuno.” Ake omwe. “Ndipo, ine ndikukuuzani inu, ife taphunzira zinthu zina kunjika uko. Iye tinaphunzira kuti Mulungu ndi wabwino kwambiri! Iye tinaphunzira ku seminare yathu kuti Mulungu ndi wabwino kwambiri! Iye samayembekezera kuti inu muchite zonse zimene Iye analemba pamenepo. Iye samayembekezera zimenezo.”

“Eya, koma,” iye anati, “Ambuye Mulungu anati.”

¹⁷⁷ Tsopano, iye akanakhala mlaliki wabwino, ngati akanakhala pa Iwo. Ndi chifukwa chake iye amatsutsidwa kuti akhale mmodzi lero. Mukuona? Muikeni iye kutali ndi izo. Kodi Amosi akananena chiyani za izo? Ine ndikanakonda ndikanamumva iye kwa maminiti faivi, ndi kujambula uthenga wake. Ine ndikanawuyika iwo pa tepi, kuti dziko lonse liwumve iwo. Uh-huh. Kenako ine ndikanakhala chete pa izo, kuyambira pamenepo mpakana. Zindikirani. Inde, bwana, iye akanazitsutsa izo.

¹⁷⁸ Ndipo zindikirani chimene iye ananena. Tsopano, Satana anati . . . Tsopano, iye sakanachita zimenezo ndi Eva, inu mukudziwa . . .

¹⁷⁹ Iye sakanachita zimenezo ndi Adamu, koma iye anachita ndi Eva. Chotero iye anati kwa Eva, tsopano, “Tsopano iwe ukudziwa *ichi*.” Iye anati, “Iwe ukudziwa, ndithudi Mulungu ndi wabwino kwambiri kuti akupweteke iwe. Mulungu . . . Iwe ndithudi sudzafa. Iwe ukudziwa Iye ndi Mulungu wabwino.”

¹⁸⁰ Iye timamva zochuluka za zimenezo lero. Iye ndi Mulungu wabwino. Koma, kuti akhale wabwino, Iye akuyenera kukhala wolungama, nayenso. Icho ndi chimene chimamupanga Iye kukhala wabwino. Iye si wachisawawa. Iye ndi Mulungu.

¹⁸¹ Ndipo tsopano, “Mulungu ndi wabwino kwambiri kuti angachite zimenezo kwa iwe.” Ndipo iye anayamba, anati, “Bwanji, iwe udzakhala wanzeru. Iwe udzakhala ndi maphunziro. Udzakhala waluntha ndi wanzeru. Iwe—iwe udzadzika zinthu zimene sukudziwa tsopano.” Mukuona?

¹⁸² Iye ankangoyenera kudziwa chinthu chimodzi, chimenecho chinali Mawu. Iye sitikusowa kuti tikhale ndi Bachelor of Art, ndi Ph.D., ndi LL.D., ndi zinthu zina zonsezi. Kungodziwa Mawu a Mulungu. Mwana wophweketsetsa, amene angakhoze kuwerenga, akhoza kudziwa zimenezo, kudziwa.

183 Koma, kulingalira, ndipo iwo anapeza chiyani? Iwo anapeza chiyani? Pomwepo iwo anasweka. Ndipo Satana anadziwa kuti iye anagonjetsa mtundu wa anthu pomwepo. Ndipo pamenepo ndi pamene iye amawagonjetsera iwo kuyambira pamenepo.

184 Ndi chifukwa chake Amosi anabwera. Chifukwa, kutchuka ndi maganizo otchuka, ndi zabwino, purezidenti wamkulu kapena mfumu, ndipo anali atabweretsa kulemera. Anthu amagulitsa miyoyo yawo chifukwa cha nyemba, monga Esau. Ine sindikuyesera kuti ndikuvulazeni, koma ndikuyesetsa kuti ndipange choonadi.

185 Inu a Democrats munagulitsa maufulu anu akubadwa osati kale kwambiri. Uko nkulondola. Ndipo sindine wa Republican. Ndine Mkhristu. Koma, m'bale, ndi chamanyazi bwanji! Ndipo anachita kutenga makina obero kuti avotere monga choncho. Koma ndi chimene Amerika ankafuna. Iwo anachipeza icho. Kawirikawiri Iye amakupatsani chimene mukufuna.

186 Mulungu, ndipatseni ine Mawu Anu. Ndi chimene ine ndikufuna. “Ndiroleni ine ndiwabise Mawu Anu mu mtima mwanga, Ambuye, kuti ine ndisakuchimwireni Inu.”

187 Oh, ena amalingalira. Koma, mwawona, Amosi sakanalingalira, chifukwa iye anali mneneri. Mawu amabwera kwa iye. Ayi.

188 Chimodzimodzi ndi Mawu lero, inu mukuyenera kuwathanthauzira Iwo, kulola Mzimu Woyera kuti uwathanthawuzire Iwo powatsimikizira Iwo mmoyo mwanu.

189 Ndi zomwe zinanenedwa, chimene, inu mukudziwa, Yeremiya ananena kwa—kwa mneneri Hananiya. Iye anati, “Pamene mneneri ameneyo ayankhula, ndipo chimene iye wanena nkuwonetseredwa, ndiye aneneri ankadziwa kuti iye amalondola.”

190 Ngati Amosi akanakhala pano, kodi inu mukuganiza kuti iye akanatani? Iye akana—iye akanakhala ndi Mawu. Ndicho chimene iye akanadzachita. Inu mukudziwa chiyani? Iye akanatiwuza ife kuti tinaphunzitsidwa mochoka ku maziko a Mawu apachiyambi a Mulungu. Iye akanatiwuza ife kuti tiri kutali ndi Mpingo woyamba wa chipentekoste. Ndi chimene iye akanadzatiuza ife Achipentekoste. Kuti, “Tsopano, iwo anali ndi pafupifupi zaka fifite kuti mudzilowetse nokha mu chochitika, ndipo inu simunafikebe pamenepo.” Oh, kodi iye akananena chiyani kwa munthu wachipembedzo? Chabwino, oh, ngati iye akanati asapereke izo, ngati iye sakanaphwasula matchalitchi, chifukwa cha makhalidwe awo oyipa, chifukwa chovomereza tizikhulupiriro, kujowina tchalitchi mmalo moti abadwiremo!

191 Chabwino, ngati inu mwabadwira mmenemo, m'bale, mlongo, iwe umachita mosinthika. Iwe—iwe umakhala ndi Mawu. Ngati Mzimu Woyera uli mwa iwe, Iwo umangodya pa Mawu okha. Yesu anati, “Munthu sadzakhala moyo ndi

mkate wokha, koma ndi Mawu onse,” osati gawo la Mawu, “koma Mawu aliwonse amene atuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu.”

¹⁹² Iye, pokhala mneneri, iye akanawona chinthu ichi mwa ife. Za . . . Amosi anali mneneri.

¹⁹³ Tsopano ine nditseka, mu miniti, koma ine ndikufuna kuti ndipange ndemanga izi zimatirire ngati ine ndingathe. Ine ndinena zimenezo, ndipo Mzimu Woyera ukuyenera kuzipanga izo kuti zimatirire. Ine ndikufuna ndikufunsemi inu chinachake.

¹⁹⁴ Ngati Amosi akanabwera kuno usikuuno ndi kudzayima pa nsanja iyi, ngati iye akanayenda chokwera ndi chotsika mmisewu ya Phoenix, iye akanawona mwa ife lero, mu zochitika za dziko lathu, mu dziko lathu la mpingo, iye akanadzawona chinthu chomwecho chimene iye anachiwona mu Samariya: chikuperekedwa kwathunthu kwa makhalidwe oyipa, kutali ndi Mawu a Mulungu. Iye akanawona gulu lachipembedzo kwambiri. Iwo anali, aliynse wa iwo, Aisraeli. Koma iye akanadzawona—makhalidwe oyipa, makhalidwe oyipa. Iye akanadzawona—iye akanadzawona kuyipa kwa anthu ndi makhalidwe oyipa pakati pa anthu. Iye akanadzawona kuyipa kwa makhalidwe pakati, pa fuko. Iye akanadzawona kuyipa kwa makhalidwe kuchoka ku Mawu. Iye akanadzawona chigololo mu mpingo. Ine sindikutanthauza . . . Eya, ziwiri zonse; chathupi, ndipo akanadzawona chigololo chauzimu. Momwe akanamatengera tizikhulupiriro ta munthu kunja kuno, ngati tizikhulupiriro ta munthu, ndi kumavomereza ito mmalo mwa Mawu, kumeneko ndi kuchita chigololo chauzimu motsutsana ndi Mulungu. Chivumbulutso 17 amanena chomwecho, kuti iwo, hule uyu, anachita tchimo, chifukwa, “Ndi zonyansa zake iye anapangitsa dziko kumwa vinyo wa mkwiyo wake.” Inde. Ife tikuwona izo zikanadzakhala pamodzi zosinthika. Iye akanadzaziwona izo, kuyipa kwa makhalidwe.

¹⁹⁵ Amosi sanaliyimbe konse boma mulandu, ngakhale. Mvetserani. Amosi sanaliyimbe konse boma mulandu, mu Malemba ake onse. Koma anawayimba mulandu anthu chifukwa chosankha boma loterolo. Oh, ine ndikanakhoza . . .

¹⁹⁶ Kodi inu mwatopa? [Osonkhana akuti, “Ayi.”—Mkonzi]. Chabwino, mungodikira miniti yokha. Mukuona?

¹⁹⁷ Musaliyimbe mulandu boma lanu. Boma silingamange nyumba pa thanthwe limene anthu avotera mchenga. Anthu akufuna zimenezo.

¹⁹⁸ Ndipo nthawi zambiri ine ndimanena zinthu pa guwa, pamene ine ndikudziwa kuti abale anga akhala kunja uko, atumiki, amuna abwino. Ine ndimayankhula nawo iwo, kuwatengera iwo pakona. Ndipo ndi ntchito yanga, podziwa zinthu izi, kuti ndiwawuze abale anga. Ndipo ndimayankhula nawo iwo. Iwo amati, “M’bale Branham, ife tikudziwa inu

mukulondola, koma mpingo wanga ungatulukemo.” Mukuona? Mukuona? Ndi chimene inu mukufuna. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. Mukuona? Iwe sungakwanitse. Ndi anthuwo.

¹⁹⁹ Tsopano, ngati inu mukuganiza kuti ine ndikhoza kuyamba kumanga kumusi kuno pa msewu ndi kugulitsa, madona lero, nsapato zachikale izo, zazitali, za zingwe? Izo mwinamwake ziri ndi chikopa chochuluka mwa izo kuposa—kuposa momwe sitolo yodzaza ili nazo lero, peyala imodzi. Koma ngati ndikanagulitsa izo masenti fifite, ndikanafa ndi njala. Chifukwa chiyani? Inu simungazifune izo.

²⁰⁰ Ngati ine nditagulitsa masiketi achikale aja, Masiketi Otaya osamangira lamba kwa akazi lero, inu mukuganiza kuti iwo angawagule iwo? Ndithudi ayi. Iwo amafuna chinachake chimene angadzikhuthuliremo, chimene chimawoneka ngati chikopa pa soseji. Iwo—iwo amangofuna zikhale zothina kwambiri. Akamayenda mu msewu, pafupifupi madigiri foro kapena faivi osiyanasiyana, atakankhidwira mkati, atakankhidwira panja, ndi kubwerera mmbuyo pa nsapato zazitali, mutu wawo utasololoka. Ndizo, sindikutanthauza zimenezo ngati nthabwala. Ano si malo ochitira nthabwala. Koma ndicho choonadi. Ine ndiribe maphunziro abwino. Iyo ndi njira yokhayo imene ine ndingapangire mawu anga, kudziwa, inu mukudziwa chimene ine ndikunena. Mukuona? Tsopano, izo nzoona. Iwo sangagule madiresi amenewo.

²⁰¹ Usiku wina pa nsanja, mkazi wamng’ono Wachimwenye anabwera pamenepo. Ine ndinkafuna kumugwira dzanja lake laling’ono. Kumtunda ku mpingo wa M’bale Groomer, kapena kulikonseko. Iye anali atavala diresi momwe mayi anga ankavalira. Ine ndinaganiza, “Chabwino, adalitse mtima wako, dona.” Ndipo Ambuye anamuchiritsa iye pomwepo, iye asanafike nkomwe kwa ine. Iye. . . Mukuona? Ine ndinaganiza, “Ine—ine—ine kulibwino ndingokhala chete.” Mukuona? “Mungodikira mpaka chochitikacho chidzabwere, nthawiyina.” Mukuona? Ndipo apo icho chinali.

²⁰² Chabwino, inu simungagulitse madiresi amenewo. Inu mukhoza kuwagulitsa iwo kwa Mmwenye, ndipo osati ochuluka a iwo. Iwo akungomasuka basi monga ena onsewo. Inu muli ndi maprogramu ochuluka kwambiri apa televizioni. Ndipo ana anu akumapitako, ndipo aphunzitsi ena a sukulu amakono awa, achizungu, akumabweramo, ndi zamkutu zina zonsezi. Inu mungakhale abwinoko, mmene munkakhallira kumbuyo uko ngati Ng’ombe Yongokhala ndi iwo anali, kalekale.

²⁰³ Mu Afrika, pamene ife tinali ndi mtundu wachikuda uko, kodi iwo amachita chiyani? Amapita kumeneko, amishonare amenewo, amakawerenga, kukalemba, ndi masamu. Pamene iye. . . Bwanji, iwo, iwo amadziwa zambiri za makhalidwe, mmafuko awo, kuposa momwe inu mungachitire, Chikristu

chikanawabweretsera iwo. Uko nkulondola. Ngati aliyense wa akazi amenewo kunja uko, ngati iye ali mu fuko la Azulu, ngati iye ayembekezera usinkhu winawake kuti akwatiwe, ndipo sanatero, winawake sanamutenge iye kukhala mkazi wake, iye ankayenera kuti achoke kumeneko. Iye samakhalanso wafuko. Ayi, bwana. Ndipo pamene iye wakwatiwa, iye amayesedwa unamwali wake. Ndipo ngati iye apezeka wolakwa, iye amayenera kumutchula mwamuna amene wachita zimenezoyo, ndipo awiri onsewo amaphedwa, limodzi.

²⁰⁴ Kungakhale kuphedwa kochuluka kuno ngati titakhala ndi dongosolo loterolo. Kodi inu simukuganiza? Izo nzoona. Iwo sangakhale ndi oyika maliro okwanira kuti akawayike amuna ndi akaziwo. Ndithudi. “Koma muli akufa, mulimonse, ndipo simukudziwa izo.” Chotero ndiro vuto lake la izo. Mukuona? Koma tsopano, mochuluka kwambiri, ndiko kulondola.

²⁰⁵ Ndiye inu mumachita chiyani? Iwo amawatengera iwo kumeneko ndi kukawaphunzitsa iwo sukulu. Kenako inu mumawapeza iwo ali pa msewu. Iwo ali nawo machimo awo a fuko, omwe iwo anali nawo; ndipo amabwera kuno, nkudzatenga machimo a mzungu; ndipo akatero iwo amakhala wagahena kuchulukitsa ka teni kuposa zomwe iwo ankayenera kuyamba nazo. Chinthu chokhacho chimene iwo akuchisowa ndi Khristu, kuti akhale pamene iwo ali. Kulondola.

²⁰⁶ Umo ndi momwe ziliri ndi Mmwenye wathu waku Amerika. Aliyense amene ine ndimamumvera chisoni, mu fuko lino, ndi Mmwenye ameneyo. Ndithudi iwo sizinawayendere mu zimenezo! Ine sindine. . .Ndine munthu mmodzi chabe, koma ine ndi wa iwowo. Inde, bwana. Ngati Ambuye adzandiyitane konse ine kuchokera ku minda, kuchita monga chonchi, ndipo uthenga wanga watha; Iye nkundilola ine kuti ndikhale moyo motalikirapo, ine ndidzapita kwa Amwenye. Inde, bwana. Inde, bwana. Mai!

²⁰⁷ Tikuwona chimene Amosi akanachita pamene iye anaitanidwa atuluke. Kachitidwe kathu konse kakanatsutsidwa. Ayi ndithu. . .

²⁰⁸ Boma silingamange (inali ndemanga yanga) pa thanthwe, pamene fukolo lavotera mchenga.

²⁰⁹ Inu mungamange bwanji mpingo wanu pa Thanthwe? Mlaliki angayime bwanji nkomwe pa guwa ndi kulalikira Thanthwe, ndi kumanga izo pa zikhazikitso za Uthenga wathunthu, pamene omvetsera ake, ena a anthu ake kunja uko, angamutulutsepo iye kunja? Tsopano, ine ndikuyimba mlandu mlalikiyo chifukwa chopanda kulimba mtima, ndi Mzimu wa Mulungu, chifukwa chongotseka chitseko, nkuti, “Mumupeze wina amene angapirire nazo zinthu zimenezo osati ine.” Ine—ine ndimasilira mlaliki amene angachite zimenezo.

210 Koma tsoka kwa osonkhana amenewo pamene munthu wodzozedwa wa Mulungu ayesetsa kuwabweretsera iwo Mawu, ndipo kenako iwo nkukanika kudzifoletsa mu mzere ndi Iwo. Uko nkulondola. Iye adzakhala bwanji ndi mpingo umene mphatso zonse naini zikugwira ntchito mmenemo, ndi zina zotero, ndipo kenako, iwo ndi izo, ndi mpingowo kulephera nkomwe—ngakhale kuti akhale mwaulemu ndi mwamakhalidwe, kulephera kuphunzira ma ABC awo a Uthenga? Ndiye nkumati, “Ngati ndikanakhala ndi mlaliki wabwinoko!” Bwanji, ndi vuto lanu. Uko nkulondola.

211 Ndi vuto la fuko lathu, Achimerika athu, kuti ife tinabwera kuno kudzafuna ufulu wachipembedzo. Kuchokera ku chiyani? Ndipo ife timabwerera mmbuyo, ndi kukayika ku likulu lathu chinthu chomwecho chimene ife tinabwerera kuno kuti tidzakhale omasuka kwa icho.

212 Fuko lino ndi lofanana kwambiri ndi Israeli. Iwo, Israeli, anabwera mu Palestina, anadzawathamangitsa okhalamowo ndipo anatenga dzikolo. Choyamba, iwo anali ndi ena abwino—abwino, amuna pa iwo. Iwo anali ndi Davide, ndi Solomoni, ndi amuna aakulu. Potsiriza, patapita kanthawi, iwo anapitiriza kumavoteramo, ndi kumakankhira mkati, ndi kumasankhiramo, mpaka iwo anakhala ndi Ahabu kumeneko, amene anakwatira wachikunja. Tsopano, Ahabu anali munthu wabwino kwambiri. Ake. . . Oh, iye—iye ankafuna kuti achite bwino, koma analephera kuti achite bwino, chifukwa cha mkazi wakeyo.

213 Tsopano, ine ndiliba kanthu kotsutsana ndi munthu amene ine ndimamukamba maminiti angapo apitawo. Iye akhoza kukhala munthu wabwino. Koma ndi kachitidwe ka hule ameneyo kumbuyo kwake, amene amapotoza khosi lake. Ndicho chinthu chimene chidzachite izo. Kubwera umo mophweka basi momwe iye angathere, monga choncho, ndi kuchitsukuluzira chinthu chonsecho pansa.

214 Kodi inu mumadziwa kuti ndi—ife tsopano. . . Ngongole yathu yadziko ndi yayikulu kwambiri, mpaka ife tikulipira ndalama zobwereka, kuchokera pa misonkho imene ife tidzalandire zaka fortini kuchokera lero. Kodi chidzachitike ndi chiyani pamene kachitidwe aka kadasweke?

215 Castro, ndithudi, ine ndimatsutsana naye iye. Iye ndi wa chikominisi. Kulondola. Ine ndimatsutsana naye iye. Koma iye anachita chinthu chabwino pamene iye anasinthana ndalama ndi kubwezeretsa golide, anagula ma bondi ndipo anabweza golideyo.

216 Ife tikuyenera kuti tichite zimenezo, kapena pali chinthu chimodzi chimene chakakamira pankhope yathu, ndicho kuti, kuti mpingo wa Katolika uli ndi chuma cha dziko lapansi. Iwo uli ndi ndalama. Iwo uli ndi golide, kuti agulenso

ma bondi athu. Ndizo ndendende. Ndipo inu mukuganiza kuti ogulitsa kachasu awa, ndi ogulitsa fodya, ndi anthu opambana a dziko sangagulitse, kuti asataye bizinesi yawo yonse ndi kuba ndalama mwachinyengo? Iwo adzabwerera mmbuyo momwe ndi kudzatenga ndalama zimenezo kuchokera ku mpingo wa Katolika, ndipo kenako iwo nkugulitsidwa. Kulondola. Kodi Baibulo silimaneneratu zimenezo, “Chuma cha mdziko”? Ine sindine wandale, kapena munthu wanzeru, koma ine ndikumuthokoza Ambuye kuti ndimamudziwa Iye. Ndipo izo nzoona. Apo ndi pamene iwo udzakhale, apo pomwe. Inu mupenyetsetse zimenezo. Inu mupenyetsetse ndipo muwone ngati izo sizooona. Basi. . . Ine ndikuyembekeza kuti ife tonse tikhala moyo kuti tidzaziwone izo, ndipo sindikuganiza kuti tikuyenera kukhala motalika kwambiri.

²¹⁷ Koma inu mudzachita bwanji? Ife tidzamanga bwanji mpingo? Ife tidzamanga bwanji fuko? Ife tidzamanga bwanji fuko pa ichi tsopano? Ife tidzachita chiyani za zimenezo?

²¹⁸ Mwinamwake ine kulibwino ndikhale chete, ndipite kwina kwake. Koma, inu mukudziwa, ine ndanena mokwanira mpaka inu mukudziwa chimene ine ndikuchikamba. Mukuona? Inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza.

²¹⁹ Tayang’anani chimene ife tikuchifuna. Inu, inu mukuona chimene inu mukufuna? Ndi chimene inu muchipeze. Ndizo zokhumba zanu.

²²⁰ Tayang’anani pa maprogramu athu apa televizioni lero, osasefedwa. Kale, zinali zolakwika kwa ana athu, ife sitinkawalola iwo kuti apite kumusi mu—mzinda ndi kukawonera kanema, zi—ziwonetsero za zithunzi. Koma tsopano mdierেকেzi anatembenuza zimenezo—ndipo anapanga izo kukhala televizioni, ndipo anaiyika iyo mnyumba iliyonse.

²²¹ Ndipo izo zingakhale zabwino, televizioni ndi yabwino, ngati mungayike chinthu choyenera pa iyo. Ndithudi, iyo ili.

²²² Koma kodi inu mumachita chiyani? Izo zikumavundiravundira pa ora, kugwiritsa ntchito dzina la Mulungu, kutukwana, kunyoza, akazi amaliseche, makhalidwe oyipa, zimenezo zimaperaka chiphe mmalingaliro a ana awa, mpaka ife tadzutsa gulu la opanda khalidwe, izo nzoona, zigawenga. Ndizo ndendende choonadi. Inu mwinanso mukhoza kuyang’ana pa izo.

²²³ Fuko lathu lonse likukhala gulu la zigawenga. Mnyamata aliyense akumayenda ndi mathalawuza ake atawakhwefulira mchiwuno mwake, ndipo mutu ukulendewera mmbuyo, ndipo tsitsi lake likulendewera mmusi mwa khosi lake monga kumeta kwa phanke kwa Akazi a Kennedy, ndi kumayendayenda monga choncho, ngati chigawenga, ndipo nkumamutcha ameneyo wa Chimerika? Inu mwagwa ku chisomo. Mulape ndipo mubwerere kwa Mulungu, kapena muwonongeka. Ndi chifukwa chake,

ife—ife tikufuna kuti tipeze winawake muno amene angatilore ife kuchita chirichonse chimene ife tikufuna kuchita. Uko nkulondola.

²²⁴ Umo ndi momwe ziriri ndi mipingo. Iwo akufuna kuti asankhe m’busa, osati m’busa amene ati adzayime pamenepo ndi kukwapula Uthenga kwa iwo. Koma iwo akufuna winawake amene angawalole iwo kuti azidzitambasulira okha mu chovala chosambira, ndi kumakasewera bunko mchipinda chapansi, ndi kumakhala moyo mulimonse mmene iwo akufunira, maprogramu apa televizioni a wayilesi yosasefedwa, zoipa ndi zonyansa, kulumikizitsa mpingo ndi dziko pamodzi.

²²⁵ Nzosadabwitsa Amosi akanakuwa motsutsa zinthu zimenezo. Inu mukuganiza kuti anthu akanamulandira iye pamene iwo akuvotera chinthucho mmenemo?

²²⁶ Ngati abusa alalikira kupitirira maminiti twente, bodi ya matrastii imamuitanira iye mchipinda ndi kukati, “Taonani kuno, abusa. Ife—ife sitinakubweretseni inu kuno kuti muzidzachita chinachake monga izo. Ife timakhala ndi programu ya maminiti twente. Pamene iwo atha, muziwusiya iwo uzipita.”

²²⁷ Chimene iye akuyenera kuchita ndi kulithamangitsira gulu la matrastii limenelo panja pa chitseko, ndi kutenga Baibulo ndi kulalikira usiku wonse, monga anachitira Paulo, ndipo anawona chiwukitsiro cha akufa. Ndendende. Iwo anamutulutsira iye panja pa nyumbayo; ngodya ya msewu ndi yabwinoko. “Mulungu ndi wokhoza mwa miyala iyi. . .”

²²⁸ Televizioni, zithunzi zosasefedwa, zonyansa, nyansi, ndi kumapangira chitsanzo. Tayang’anani pa ana athu achichepere lero. Tayang’anani pa atsikana athu. Muwone ana aang’ono akubwera kuchokera ku sukulu, osapitirira usinkhu wa zaka sikisi, seveni, eyiti, akuyatsa ndudu. Nchifukwa chiyani ziri chomwecho? Amayi awo pambuyo pawo mwina ankachita zimenezo. Ngati iwo sankachita zimenezo, ndiye kuti ana ena amene iwo akucheza nawo. Muziwona amene ana anu amasewera nawo. Kulondola. Kuno lina. . .

²²⁹ Nthawi ina kale, mkazanga akudziwa zimenezo, ife tinali titakhala pa tebulo. Ndipo Joseph wanga wamng’ono anatulutsa mawu amene akanapangitsa woyendetsa panyanja woledzera kudzichitira yekha manyazi. Ine ndinatembenuka. Ine ndinati, “Chimenecho ndi chiyani?” Ndipo amake anali ngati kuti akomoke. Mnyamata wamng’ono anawoneka wosalakwa.

²³⁰ Iye anati, “Chavuta ndi chiyani, adadi?” Ndipo misozi yayikulu mmaso mwake.

²³¹ Ine ndinati, “Usadzanenenso chinthu choterocho.” Iye sankadziwa chimene icho chinali. Ndinadzazindikira kuti, ana ku sukulu ankagwiritsa ntchito mawu onyansa amenewo. Ine ndinati, “Wokondedwa, izo ndi za mdierekezi.”

232 Mwaona, ndi zimenezotu, ana anu. Izo zangofika pamalo, m'bale, mpaka zangokhala galu-kudya-galu, chipwirikiti choterocho cha tchimo. Oh, mai! Maprogramu a pa televizioni, okonda-tchimo, okonda-zosangalatsa! Oh, mai!

233 “Maminiti twente ndi nthawi yotalika mokwanira. Ine ndiyenera ndikawonere kanema yochedwerapo.” Mukuona? “Fulumirani ndipo muchichotse ichi muno. Ine ndikuyenera kuti ndichite zimenezo.” Mukuona? Iwo achita chipembedzo chawo. Iwo anapita kumusi uko, ndipo izo ndi zokwanira.

234 Koma, ine ndikukuuzani inu, mwamuna weniweni kapena mkazi amene wabadwa mwa Mzimu wa Mulungu adzakhala ora ndi ora, akumwa mu Mawu a Mulungu. Osati zokhazo, koma pamene izo zifika pamenepo, izo zimakhazikika ndi kusintha moyo. Amen. Inde.

235 Ndi zokhumba za anthu athu. Kachitidwe kathu konse kavunda ndipo kawonongeka. Ndi zofuna za anthu athu.

236 Inu mumutenge mwamuna wabwino, mwina, ngati mwamuna wabwino, mukamuyike iye mu banja limene liri gulu la okonda-zosangalatsa, iwo adzamutsogolera mwamuna ameneyo moyo wa galu; kapena, mkazi wabwino, mmodzi aliyense, kuwayika iwo m'banja limene lasokonezeka. Bwanji, banja lonse likuyenera kudzipereka kwa Mulungu. Ndi ntchito yathu kuti tizipemphera, mpaka ana athu atapulumutsidwa, tiziyika nyumba yathu mu dongosolo. Eya.

237 Ndife chinachake monga Israeli anachitira, amene anapanga mgwirizano ndi adani awo. Choyamba, iwo ankayenera kuchoka ku Mawu iwo asanachite zimenezo. Ndipo izo zikungowonetsera momwe Amerika yapitira kutali ndi Mawu.

238 Inu mukudziwa, inu—inu mukuyenera kukana choonadi musanakhulupirire bodza. Uko nkulondola. Ndizo ndendende. Eva poyamba nkayenera kukana Mawu a Mulungu asanatenge bodza la Satana. Iwo ankayenera kuchoka ku Mawu ndiye, chimodzimodzinso lero, kulola kuti Rome atenge ulamuliro popanda kuwombera. Iwo sakuwadziwa Mawu a Mulungu pa zinthu izi. Ndiro limene liri vuto lake.

239 Ife tikusowa kuwuka kwa mneneri woona, kuti atibwezeretse ife ku Mawu. Uko nkulondola. Ife tinalonjezedwa mmodzi. Ife tinalonjezedwa zimenezo. Inde, ndithudi. Malaki 4 anati iye adzatero. “Ndipo iye akanadzabwezeretsa Chikhulupiro cha anthu kubwerera kwa atate achipentekoste amenewo kachiwiri.”

240 Amosi ankadziwa kuti achikondi opanda umulungu a Israeli akanadzamuwononga iye tsiku lina. Tsopano ndiroleni ine ndinene izi molemekeza. Wokhulupirira amadziwanso lero kuti dziko, a Achimerika awa okonda opanda umulungu, amuwononga iye. Chikondi chanu cha ndale! Ine ndingozisiya izo zizikike miniti. Izo zidzawononga fuko. Ndipo chikondi

chanu cha mdziko, chosamabwera ndi Mawu ndi kuchita chimene chiri cholondola, chidzawononga mpingo. Ndiko kulondola ndendende. Ndikukhulupirira kuti zimenezo zamveka. Mpingo unali utamusiya Iye, unasiya Mawu Ake a Moyo. Dziko lonse limapunthwa pa iwo, ngati chopunthwitsa. Iwo akuchita chinthu chomwe chomwecho lero. Inde. Ngati Amosi akanakhala pano, iye akanafuula motsutsa kachitidwe konseko.

²⁴¹ Tsopano, potseka, ine ndikufuna kuti ndinene ichi, mu ndime 8. Mvetserani mwatcheru. Iye anati, “Mkango ukabangula, ndani koma amene angawope pamene mkango ubangula?”

²⁴² Ndipo ine ndasakapo mikango. Mkango ndi mfumu ya zirombo. Mu Afrika ine ndagonapo uko mu zipululu zimenezo, pa nthawi ya usiku, pansi pa udzu wawung’ono umenewo, kapena iwo unali wobaya.

²⁴³ Mkango umalumphira pamaso pa mfuti yowombera. Iwo sumawopa izo, koma iwo sungafike pafupi ndi minga. Inu munamvapo nthanoyo. Koma, izo nzoona, mkango sumafika pafupi ndi minga. Iwo amamanga nyumba zaminga monga choncho, ndipo mkango sumalumphira pa iyo. Apo ayi, iwo ukhoza kufika, nkulowa mmenemo.

²⁴⁴ Billy ndi ine. Ine ndikukumbukira nditagona kunja uko usiku wina, ndipo ndinamva kamwa lake lalikulu lakale likuphokosera, kutali *uko* ndi mutu wanga, mwawona, koma iwo—iwo sukanafika pafupi. Phazi lake lalikulu lakale, pafupifupi monga *choncho*, ukuyenda mozungulira pansi.

²⁴⁵ Ndipo iwe umakhoza kumamva chirichonse kuchokera kwa afisi, fisi akuseka, fisi wolira, ndipo—ndipo iwo—akukuwa. Ndipo—ndipo iwe nkumamva ankhwere, anyani, ndi—ndi nswala, ndi njovu ndi kulira konyinyirika kumeneko ndi “whiii.” Iwe umakhoza kumamva izo kwa mailosi. Ndipo nsikidzi ndi akafadala zamitundumitundu zikupanga phokoso lawo. Koma mungolola mkango ubangule cha patali, ngakhale akafadala amasiya kufuula. Iwo amamvetsera. Chifukwa chiyani? Ndi mfumu yawo. Iwo amamvetsera kwa iyo.

²⁴⁶ Baibulo linati, “Pamene Mulungu...Pamene mkango ubangula, ndani amene sangawope? Ndipo pamene Mulungu ayankhula, tingakhale bwanji osanenera?” Kodi tingapewe bwanji izo? Pamene Mulungu ayankhula, mneneri amafuula Mawu olankhulidwa. Ndipo ngati Iwo ali Mawu a Mulungu . . .

²⁴⁷ Ndipo mkango ukabangula; akafadala, chirichonse, chimatonthola, chifukwa iwo amachita mantha. Yawo—yawo—mfumu yawo ndi—ikuyankhula. Izo zimakhala ndi—nzeru zokwanira, kulimba mtima, ndi ulemu wokwanira, kuti azilemekeza mfumu yawo pamene iye akuyankhula.

²⁴⁸ Chotero, Mulungu amayankhula mwa Mawu Ake, ndipo amalola cholengedwa chirichonse cha chirengedwe Chake

kuti chisamalitse. Iye akuyankhula mmasiku otsiriza ano. Iye akupereka Mawu Ake. Ndipo cholengedwa chirichonse chimene chiri mu Ufumu Wake chisamalitse chimene Iye akunena. Chiyime. Chifufuze. Iye akubangula tsopano, akubangula mwa Mawu Ake otsimikiziridwa. Iye akuzizindikiritsa Yekha. Pamene Iye akubangula mmasiku otsiriza ano, tiyeni tisamalire, ndi kudziwa kuti pali chinachake chikukonzekera kuti chichitike, kumadziwa kuti Mulungu samachita kose zimenezo popanda Iyeyo kubangula poyamba. Pamene Iye abangula, ndiye chinachake chimatsatira kubangula kumeneko, inde, chifukwa Iye akubwera pamenepo.

249 Iye anati, “Kodi a—a . . . Kodi mkango ubangula tsopano popanda chifukwa? Kodi mkango wawung’ono umalira, kuchokera mu mphanga, iwo usanadye kalikonse?” Mukuona?

250 Mulungu amakhala ndi chifukwa chobangulira, chifukwa Iye amadziwa kuti chiweruzo chayandikira. Ndipo, Mawu Ake, Mawu Ake ndi mneneri. Iye ali. “*Uwu* ndi ulosi wa Yesu Khristu.” Ndi vumbulutso, Mulungu kudziwulula Yekha kwa ife kudzera mu Mawu Ake olembedwa. Ndipo Iye ndi Mawu. Ndipo, tsopano, *awa* ndi Mawu Ake. Palibe chimene chingawonjezedwe kwa Iwo kapena kuchotsedwa kwa Iwo, koma Iwo akuyenera kukhalidwa moyo ndi kuwongoledwa momwe Iwo aliri. Iye sitingayerekeze, kuchotsa chirichonse kwa Iwo kapena kuwonjezera chirichonse kwa Iwo. Mulungu akanali Mulungu. Iye akubangula.

251 Iye anati, “Monga izo zinali mmasiku a Nowa, chomwechonso izo zidzakhala mu kudza kwa Mwana wa munthu. Iwo ankadya, kumwa, kukwatira, kukwatiwa, makhalidwe oyipa.”

252 “Ndipo monga zinali mmasiku a Loti,” Iye anabwera Yekha mu thupi la mnofu, ndipo anadzazitsimikizira Yekha kukhala pamenepo kwa Abrahamu. Anati, “Chomwecho zidzakhala mu kudza kwa Mwana wa munthu.” Yang’anirani zinthu izi. Kuwala kwa kumadzulo kukuwala.

253 Oh, ngati ife tikanakhala ndi Amosi powonekera lero, kumulola iye abangule, iye akanadzazira kachitidwe kathu ndi miyambo yathu, ndipo Mawu a Mulungu akanakwera mwachigonjetso.

Tiyeni tipemphere.

254 Atate Akumwamba, yankhulaninso. Bangulani, Ambuye, ndi Mzimu Woyera. Iye ndi Mneneri wa orali. Iye ndi Mneneri wa tsikuli, akuyesera kuti apeze njira Yake mmitima ya amuna ndi akazi, kuti Iye adzathe kuyankhula Choonadi. Ndine wokondwa kuti Iye akuwapeza ena. Ine ndikupemphera, Atate Akumwamba, kuti Iye adzapeze ambiri muno usikuuno, kuti Iye adzakhoze kumugwiritsa ntchito winawake amene ali wokonzeka kukhala wolemekeza. Pamene iwo adzamva

kubangula kwa Mulungu wamphamvuzonse kukupita mwa Mawu Ake, chiweruzo chayandikira.

²⁵⁵ Pamene mkango ubangula, iwo ukubwera. Chirichonse—cholengedwa chirichonse chimadziwa kuti ndibwino chibisale, chifukwa mfumu ikupita patsogolo.

²⁵⁶ Mulungu, ife tiri ndi malo amodzi okha otetezeka, pamene Mfumu ya mafumu ikubangula, ndiwo Magazi a Yesu Khristu. Ife tiri nawo malo otetezeka. Ine ndikupemphera, Atate Akumwamba, kuti Inu muyankhule kwa mitima usikuuno. Ndipo mulole iwo adziwe kuti iwo akukhala mmithunzi ya Kudza kwa Khristu, pamene mafuko akusweka, ndipo zinthu zikuchitika, za chimene iwo ali. Ndipo, komabe, mu chifundo Chanu chanthete. . .

²⁵⁷ Ife tachimwa kwambiri, zikuwoneka ngati Inu mungatembenezire nsana Wanu kwa ife, ndi kutilola ife kuti tichokepo. Koma, apobe, monga Inu munali kumbuyo uko mu Edeni, Inu mumapanga njira yothawirapo. Inu munapanga njira yopulumukira kwa Nowa. Inu munapanga imodzi kwa Mose, ndi kwa Daniele, ana Achihebri. Inu, Inu mosalekeza mukumapanga njira. Ndipo iwo amene amayipeza Iyo, iwo amayenda mu Kuwala kwa Mulungu ndipo amakhala ndi Moyo. Iwo amene amaikana Iyo, amatsutsidwa ndipo amaponyedwa kutali.

²⁵⁸ Ine ndikupemphera, Atate Akumwamba, pasakhale aliyense wa iwo muno usikuuno, amene aponyedwere kutali. Mulole iwo mokoma amve kubangula kwa Mulungu, Mzimu Woyera ukuyankhula pansu mmitima yawo, ndipo ukuti, “Uyu ndi Ine. Musawope ayi. Ndi Ine.” Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

²⁵⁹ Ine ndisiya kuyitanira kuguwa kwa pafupifupi maminiti teni. Ine ndachedwa pang’ono. Koma ndikukhulupirira Billy anapereka makadi apemphero mausiku angapo apitawo, kapena chinachake chimzake, uko kwa M’bale Groomer. Ndipo ine ndikuganiza iye wakhala akuwapereka iwo usiku watha. Ine sindinawayitane konse iwo. Ine sinditi. . . Ine ndikuganiza iye anawapereka iwo kachiwiri usikuuno. Ine sindikudziwa ngati iye anatero kapena ayi, koma tiyeni tiyitane ena a makadi amenewo. Kodi M’bale Groomer ali pano? Groomer? Ayi, ayi. Groomer. Kodi iye ali pano? Kodi ife tinayambira pati? Tinayambira nambala. . . Kodi ife sitinayambire pa nambala wani, kumtunda uko?

²⁶⁰ Usiku wathawu, tinalibe makadi apemphero. Ife. . . Mzimu Woyera unangopita kudutsa mwa omvetsera ndipo unawayitana anthu. Kodi mukuzikonda zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Ine ndikutero, nanenso. Ndipo kulalikirira mwamphamvu monga chonchi, kuti mwinamwake ndikulekerera pang’ono pa izo.

²⁶¹ Ine—ine ndikawapatsa anthu khadi la pemphero, ine ndimakhala wokakamizika kuti ndimupempherere munthu ameneyo. Ndizo zonse. Ngati ife tiribe kuzindikira kulikonse, izo ziri bwino. Koma ndine wokakamizika kumupempherera munthuyo. Mwana wanga amapereka khadi la pemphero, ine—ine ndikuyenera kuti ndimupempherere munthu ameneyo. Ndizo zonse. Chotero, ine—ine ndikumverera chomwecho. Ine ndichita zimenezo, Mulungu akandithandiza ine. Ndisanachoke mdziko muno, ine ndi—ine ndichita zimenezo.

²⁶² Tsopano, sitingatenge nthawi yayitali kwambiri. Tiyeni tiwone, ife tinayambira pa wani mpaka twente-faivi, ine ndikukhulupirira izo zinali, usiku umenewo. Eya, wani mpaka twente-faivi. Ine... M'bale Groomer, kodi muli pano? M'bale Groomer? Ine sindimatchula ilo molondola. Koma ine ndikuganiza ndiko kulondola. Wani... .

²⁶³ Chabwino, tiyeni tiyambire penapake usikuuno. Tiyeni tiyambe, tiyeni tiyambire sevente-faivi, kenako, mpaka wani handirede. Amene ali ndi khadi la pemphero nambala sevente-faivi, kwezani mmwamba dzanja lanu. Tiyeni tiwone ngati... . Chabwino, uko nkulondola. Izo nzabwino. Chabwino, bwerani kuno, dona. Sevente-faivi, sevente-foro, sevente-...sevente-faivi yokha. Tsopano sevente-sikisi, sevente-seveni, sevente-eyiti, sevente-naini, eyite, eyite-wani, eyite-thuu, eyite-firii, eyite-foro, eyite-faivi, eyite-sikisi, eyite-seveni, eyite-eyiti, kupitirira mpaka wani handirede. Aloleni iwo abwere kuno. Billy Paul ali kuti? Pepani. Chabwino. Katenge, pita kumusi uko. Othandizira ena amuthandize iye mpaka iwo alowe mu mzere wa pemphero.

²⁶⁴ Tsopano, nonse a inu, yang'anani kwa ine miniti yokha. Eya. Kodi inu mumamukonda Iye? Tiyeni tingoyimba modekha, mokoma, miniti yokha, pamene ena a inu abale othandizira mukupita kumeneko. Oh, zikomo inu. Iwo ali nawo, kumusi uko, chotero iwo... . Kuchitira kuti mizere isasakanizidwe. Ine ndikufuna kuti ndiwapempherere anthu awa. Ndiye, mawa, ife mwinamwake tidzakhala tikupempherera odwala chimodzimodzi basi, ndi kumapitirira ndi kumapitirira, mpaka msonkhano wawukulu udzayambe. Ndipo ine... .

²⁶⁵ Mwinamwake M'bale Roberts akhoza kukhala ndi mzere wa pemphero kumtunda uko, nayenso, kumtunda ku—ku malo. Ine ndimaganza mwina awiri tonse tikhale ndi umodzi pamodzi, wina mbali imodzi, ndi wina kwina. Koma ine—ine sindikudziwa ngati iye angakonde zimenezo kapena ayi. Ine sindinayankhule naye iye, ndipo ine kulibwino ndiyankhule naye poyamba, inu mwawona. M'bale Oral ndi m'bale wabwino, ndi wantchito weniweni wa Khristu. Ndipo iye angakhale wodzichepetsa mokwanira kuti achite izo, koma ine ndimakhala ngati ndimadana ndi kudziponyera ndekha mmenemo ndi mwamuna wonga ameneyo, inu mwaona. Chotero ine mwina

kulibwino ndizisiye izo zokha. Chabwino, ngati iye angandiuze ine, ngati iye angandipemphe ine, “M’bale Branham, bwerani mudzandithandize ine,” ine ndinga—ine ndingakhale wokondwa kuchita zimenezo. Koma, tsopano, iye ndi m’bale wodzichepetsa ndi wokoma kwambiri. Ndipo ngati iye angandifunse ine kuti ndichite zimenezo, ine, ndithudi, ine ndingachite izo. Koma ndingafune kuti iye andifunse ine, poyamba, inu mwawona. Ine kulibwino ndisanene kanthu za izo. Inu musati mukatchule izo kwa iye, tsopano. Basi mungozisiya—mumusiye iye andifunse ine, ndiye ine ndidziwa kuti ziri bwino. Mukuona?

²⁶⁶ Koma tsopano—tsopano ife tiwona. Ndi angati atenga... Chabwino, tsopano, tiyeni tiwone. Ndi makadi apemphero angati omwe ali mchipinda muno? Tiyeni tiwone manja anu. Oh, pali enanso owonjezera, mwina fifite owonjezera. Forte, fifite owonjezera, mwinamwake. Oh, eya, mwinamwake sarte owonjezera. Chabwino. Tsopano tipeza—tipeza...

²⁶⁷ Ife tiwatenga iwo. Tsopano ndife... Mungogwira khadi lanu, ngati simunaitanidwe. Mwawona, ndi maminiti teni itadutsa teni, ndipo ine—ine ndikufuna inu mudzakhale pa Sande sukulu mmawa. Ndipo mwinamwake mawa, pokhala ndi misonkhano iwiri, tikhoza kudzachotsa pafupifupi makadi onse amene tiri nawo pamene, ndipo kenako—kenako nkudzayambanso mwatsopano Lolemba.

²⁶⁸ Kodi tidzakhala kuti Lolemba usiku? Oh, ife tidzakhala kumusi, titi, ku Tucson. Musadzaiwale kubwera ku Tucson tsopano, ku msonkhano wawukulu kumusi uko. Aliyense muno wochokera ku Tucson? Eya. Zedi. Munda wa mdziko, ndithudi, inu mukuyenera kukhala ochokera kumeneko. M’bale Carl Williams adzanditsatira ine chifukwa cha zimenezo, ena a masiku awa. Pamene ine ndinabwera kuno koyamba, iyi inali mizinda yopikisana, ndipo ndikuwona kuti ikanali.

²⁶⁹ Ine ndinazolowera zimenezo. Ya mpira yathu, besibolo, kapena timu ya basiketibolo kwathu, mizinda yopikisana imeneyo, Jeffersonville ndi New Albany, oh, mai, mai, mai! Psyii! Sipakhalapo usiku umene sikumakhala kulimbana kwakukulu, iwo akakhala ndi masewera, ndiye sindikudziwa kumene izo zingakhale.

²⁷⁰ Iwo amakhala mosalekeza pa izo, ine ndikudziwa, mu Tucson. Koma Phoenix yakula kuposa Tucson nthawi zambiri, ine ndikukhulupirira, chifukwa ine... Tucson, ine sindikuganiza kuti ndi gawo limodzi mwa magawo atatu a kukula kwa Phoenix. Koma...

²⁷¹ Ife tikupita kumusi uko, chifukwa iwo ali ndi anthu abwino, oyera kumeneko, ine ndikutsimikiza. Kulikonse kumene ine ndimapita mdziko, mpaka mu nkhalango za ku Afrika, ine ndimaphezabe zimenezo. Oh, mai! Ine ndikanakonda ndikanamubweretsa mkazi wanga kuno kudzakuimbirani inu

nyimbo ija usiku wina, “Iwo amabwera kuchokera Kummawa ndi Kumadzulo, kuchokera ku mayiko akutali.” Tsopano, iye adzuka ndi kuzemba pamene ine ndanena zimenezo.

²⁷² Chotero, iye akuchita mantha kwambiri ndi M’bale Rose. M’bale Rose anati, “Mlongo Branham ali pano. Ife timubweretsa iye kuno, adzanene mawu amodzi.”

²⁷³ Iye anati, “Mtima wanga unalumpha pafupifupi kulumpha ka fifitini.” Anati, “Ndinagwetsera mutu wanga pansi.” Anati, “Bill, ngati iye ali paliponse mu msonkhanowu,” anati, “Ine ndikutsimikiza ndibisala.” Iye ndi wotsalira mmbuyo weniweni. Chotero, ine—ine—ine ndikamva izi ndikakafika kunyumba.

²⁷⁴ Ine ndikuyembekeza kuti nonse achinyamata...Ine ndikunena izi, osati chifukwa iye ali pano. Inu mukudziwa zimenezo, ndi onse amene akumudziwa iye. Ine ndikuyembekeza kuti mnyamata aliyense mchipinda chino, pamene iye adzakwatira mkazi wake, kuti iye adzakhala wokoma kwa iye, ndipo inu mudzakhala osangalala limodzi, monga momwe ine ndi mkazi wanga takhalira zaka izi. Ngati pali kuyamikira kulikonse koti kuperekedwe kwa banja la a Branham, mulole iko kupite kwa iye. Iye ndi mfumukazi. Iye ndithudi ali. Chinthu chimodzi, iye ndi mayi weniweni. Ndiyeno taonani zimene iye amayenera kupirira nazo, mwawona, ndiyeno, chabwino, inu munga—mungadabwe kuti izo ndi chiyani. Bwanji, anthu pakhomo, usana ndi usiku. Ndipo iye amayima pakati pa ine ndi anthuwo, mwawona, uko ndi kumene, kwathu. Chotero imeneyo ndi ntchito yovuta kwenikweni.

²⁷⁵ Ndipo Billy Paul wamng’ono, ine ndimaganza za, nthawi zambiri, ine ndinkamunyamula iye, pamene amayi ake anamwalira, basi mwana wamng’ono. Dr. Adair anakonda kunena, “Ndiwe munthu wachilendo.” Ndipo ine ndimakhala uko pa msewu, nditamunyamula iye, ndipo iye akulirira amayi ake, ndipo kunja kukuzizira, inu mukudziwa, ine nditamunyamula iye pa phewa langa, monga *chonchi*.

²⁷⁶ Ndipo ndinalibe ndalama zokwanira kusunga zake... kapena kumupezero iye botolo lenileni. Ine ndinali ndi botolo la Kokakola la iye lokhala ndi nsonga pamwamba pake. Ndinkaliyika ilo *umu*, ndi kulisunga ili mnkhwapa mwanga, kuti lizitentha. Iye akayamba kulira kwambiri, ine ndinkangofikira, ndikuyika nsongayo mkamwa mwake. Kumulola iye ayamwe kanthawi pang’ono, ndi kulibwezeretsa botololo pansi *apa*. Ndipo ndimakhala ndi mkaka paliponse pa ine, ndi chirichonse, inu mukudziwa.

²⁷⁷ Ine ndimakhala nditamugwirizitsa iye, kumapitirira, inu mukudziwa, kumunyamula iye. Nthawi yausiku, mai, mai, momwe ine ndimayesera kumugwedeza iye kuti agone, ndi kupeza winawake kuti abwere adzamuyang’anire iye pamene ine

ndinkapita ndi kukapempherera odwala. Ife tachokera kutali limodzi. Ndikuyembekeza Iye atisunga ife mwanjira imeneyo.

²⁷⁸ Ine ndinamuwona iye dzulo, atanyamula mnyamata wake wamng'ono. Ndipo ine ndinaganiza, "Billy, ameneyo unali iwe, kanthawi pang'ono kapitako." Chabwino, umo ndi momwe ife tiyenera kuchitira, kuchoka panjira, ndi kuwapatsa ena mwayi. Lidalitsike Dzina la Ambuye.

²⁷⁹ "Pamene mkango ubangula, mwawona, ndani amene sangawope?" "Ndipo kuwopa Mulungu ndi chiyambi cha nzeru." Kulondola uko? Icho ndi chimene munthu wanzeru ananena. "Kuwopa Mulungu."

²⁸⁰ Tsopano, ine ndikufuna inu anthu mu mzere wa pemphero uwo, mwayima pamene, nonse inu amene mukudziwa kuthi ine sindikudziwa kanthu za inu, kwezani mmwamba manja anu. Aliyense. Ambuye wabwino Wakumwamba pokhala Woweruza wanga; momwe ndikudziwira mmoyo wanga, sindinawonapo mmodzi wa iwo mmoyo wanga. Iwo mwinamwake anandiwonapo ine, atakhala uko mwa omvetsera.

²⁸¹ Tsopano, ndi angati kunja uko mwa omvetsera, amene akudziwa kuthi ine sindikudziwa kanthu kamodzi kokhudza inu? Koma, komabe, inu mukudwala, ndipo inu mukukhulupirira kuthi, Mulungu, inu mukhoza kugwira mphonje ya chovala Chake, ndipo Mulungu akhoza kuyankhula kwa ine kuthi ndikuitaneni inu, monga Iye anachitira ndi mzimayi, monga mzimayi wapachiyambi? Oh, mai! Nzosadabwitsa ndinalalikirira motalika chotere. Omvetsera monga choncho, ali ndi chikhulupiriro cha mtundu umenewo, zikuyenera kuchita zimenezo.

²⁸² Dona uyu? Tsopano, apa pali dona. Ife takomana usikuuno ngati alendo, ndipo tsopano iye wayima apa. Ndithudi, mwinamwake iye akudwala, kapena iye akhoza kukhala ndi vuto lina.

²⁸³ Mwaona, Mulungu amachita zinthu zina pambali pa kuchiritsa odwala, inu mukudziwa. Ndipo chotero. . . Ndipo Iye analonjeza kuthi adzakwaniritsa zosowa zathu zonse, zosowa zathu, nthawizina osati zofuna zathu, koma zosowa zathu. Tsopano ine ndikufuna kuthi mungoganiza, mmodzi tsopano, mukapita kwanu, kapena ngati simunawerengapo zimenezo, mukawerenge Yohane Woyera 4, ndi—ndipo mukawone tsopano. Tsopano, apa, tsopano, ine sindikukumbukira. . .

²⁸⁴ Ndiroleni ine ndinene ichi. Ine ndikukhulupirira, utumiki uwo, mwina Iye anditengera ine kwathu kapena adzawutengera iwo mmwamba. Ndi—zafika mpaka ku nthawi yotsiriza iyi. Kapena, mwina kunditumiza ine kutsidya kwa nyanja kapena kwina wake kumene iwo sanamvepo Izo. Mukuona? Pali chinachake chikukonzekera kuthi chichitike. Inu mungokumbukira.

²⁸⁵ Ndipo, mvetserani, ine siwogulitsa matepi. Koma ine ndiri ndi m'bale wabwino pano amene amatenga matepi awa, ndipo ameneyo ndi Bambo Maguire. Ine ndikukhulupirira kuti ndi James Maguire. Ndipo ake—apongozi ake, M'bale Sothmann kumbuyo uko, iwo ali ndi matepi amenewa. Ine ndikanati, ngati aliyense wa inu muli ndi tepi rekoda. . . Ine sindinena kalikonse za izo tsopano, chifukwa ine sindikudziwa kanthu za izo. Koma ngati inu munayamba mwagulapo tepi kwa iwowo, kaguleni tepi imeneyo, *Mabwana, Ndi Nthawi Yanji Ino?* Mukaimvetsera iyo, *Mabwana, Ndi Nthawi Yanji Ino?* Mukaisewere iyo mwapemphero, ndipo kenako mudzayamba kundipempherera ine. Mukuona? Pamene inu. . . Chifukwa, mudzawona pamenepo—vuto limene ine ndayimamo pano usikuwuno. Kukamba za mu vuto, ngati inu mukanadziwa zomwe ine ndikuyimira, pompano, pomwe pano! Mukuwona? Koma ndikuyenera kupitirira. Wopambana samasiya, ndipo wosiya samapambana. Uko nkulondola. Ndikuyenera kuchita chimene ndalalikira. Mukuwona? Tsopano, ine ndikumukhulupirira Mulungu. Ine ndikumukhulupirira Iye pakali pano.

²⁸⁶ Tsopano, apa ndi pamaziko. Tsopano, ngati ine—ngati ine ndikanakhala Ambuye Yesu wathu nditayima pano, ndipo mkazi uyu anali akudwala, inu mukudziwa ine sindikanamuchiritsa iye ngati ine ndikanakhala Ambuye Yesu. Ine sindikanachita izo, chifukwa ine ndinali nditachita kale izo. Tsopano, ndi angati akudziwa kuti izo nzoona? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Mukuona? Ndithudi.

²⁸⁷ Iye wakhululukira kale tchimo lirilonse. Iye wachiritsa kale munthu aliyense wodwala. Iye anatengera kale Magazi amenewo pa Kalvare. Mtengo walipidwa kale. Zonse zalipidwa. Koma chinthu chokha chimene inu mukuyenera kuchita ndi kuvomereza Izo, kukhulupirira Izo ndi kulandira Izo. Ndipo inu simungathe kulandira Izo mpaka poyamba mutakhulupirira Izo. Mukuwona? Khulupirirani Uthenga.

²⁸⁸ Tsopano, koma bwanji ngati Iye akanayima apa, atavala suti iyi imene Ambuye wabwino anapangitsa M'bale ndi Mlongo Williams kundigulira ine, pafupifupi zaka faivi kapena sikisi zapitazo? Ndipo bwanji ngati Iye akanayima pano chifukwa cha suti imeneyo, atavala suti iyi, ndipo mkazi uyu anali atayima apa?

²⁸⁹ Tsopano, ngati Iye akanakhala ndi zipsera mdzanja Lake, Iye akanati, “Mwawona, ine ndi Mesiya. Ine. . . Mukuwona zipsera? Yang'anani pamphumi Panga.” Tsopano, wonyenga aliyense akhoza kuchita zimenezo. Uko nkulondola. Sakanamudziwa Iye ndi zimenezo. Ndipo ngati Iye akanayima apa monga choncho, ine ndikanadziwa kuti sanali Iye. Ndikanadziwa kuti sizinali.

²⁹⁰ Chifukwa, pamene Iye abwera, lipenga lidzawomba.

Ife tidza...Iye sadzabwera konse ku dziko lapansi. Ife tidzakwatulidwa mlengalenga, kuti tikakomane ndi Iye. Mukuwona? Ife timamugwira Iye mlengalenga. “Ife amene tiri moyo ndi kutsalira tidzakwatulidwa pamodzi ndi iwo, kukakomana ndi Ambuye mlengalenga.” Iye sadzabwera pa dziko lapansi. Ife tidzakomana Naye mlengalenga.

²⁹¹ Koma tsopano, Iye anati, “Ine ndidzakhala ndi inu, mpaka mapeto a dziko. Ine sindidzakusiyani kapena kukutayani inu.” Iye angakhale bwanji? Moyo Wake. Ndiye, ngati Moyo Wake ukanakhala mwa ine, ndipo kenako ine ndikanamuyimira Iye. Kenako, ngati izo zikanati, iwo ukanakhala Moyo womwewo umene unali mwa Iye, iwo ukanachita zinthu zomwezo zimene Iye ankazichita.

²⁹² Tsopano, apa pali mwamuna ndi mkazi, monga Yohane Woyera 4. Iye anakumana ndi mkazi. Iye sanamuwonapo iye kale. Iye anali asanamuwonapo Iye. Ndipo apo iwo anayima, pamodzi. Ndipo Iye anamuwuzi iye, mkazi pa chitsime, chimene vuto lake linali. Ndipo pamene Iye anachita izo, iye anati, “Bwana, ine ndikuzindikira kuti Inu ndi—Inu ndi mneneri.” Iye anati, “Koma ife tikudziwa kuti Mesiya, Iye akadzabwera, Yemwe amatchedwa *Khristu*, amanthawuza, ‘Wodzozedwayo’; pamene Iye adzabwera, Iye adzachita zinthu izi, kuti wuzi ife zinthu izi.”

Ndipo Iye anati, “Ine ndi Iye, amene akuyankhula ndi iwe.”

²⁹³ Tsopano, ngati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse; kokha, thupi logwirika...Iye amagwiritsa ntchito thupi lathu. “Iye ndi mpesa. Ife ndi nthambi.” Kenako, Mzimu umenewo ukanachita kachiwiri chimodzimodzi basi monga Iwo unachitira pamene Iwo unali mwa Iye. Ndi kulondola uko? Kodi izo zingakupangitseni inu kukhulupirira? Nenani, “Ameni,” ngati izo zingatero. [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi].

²⁹⁴ Tsopano, dona, ine posakudziwa iwe, sindinakuwonapo mmoyo wanga, monga ine ndikudziwira. Zowona, mwinamwake iwe unandiwona ine pa msewu kapena mmisonkhano, ndi zina zotero. Koma ino ndi nthawi yathu yoyamba kukumana.

²⁹⁵ Tsopano, ngati—ngati ali machiritso amene iwe ukuwafuna, chabwino, ine, ngati ine ndikanatha kuchita izo, ine ndikanatero, ndipo ngati ine ndikanakhala ndi njira iliyonse. Ndipo ngati ziri zachuma, ngati ine—ine ndikanatha kuthandizira izo, ine ndikanachita izo. Ndipo ngati inu munganene, mwina akhoza kukhala wina, inu munganene, “Ine ndabwera kuno, M’bale Branham, kuti inu mupempherere—mwana wanga wamwamuna, kapena mwana wanga wamkazi, kapena mlongo wanga, kapena abambo,” kapena winawake. Ine ndikanachita izo, mwawona, chirichonse chimene ine ndikanatha.

296 Ndipo—ndipo ngati inu mukanakhala ndi vuto la m’banja, ine ndikanati, “Ndikufuna kukumana nanu ndi amuna anu, pamodzi, ndi kuyankhula nanu kwinakwake pambali pa kuno, inu mwawona, kuti ine ndithe kuyankhula kwa inu nonse awiri ndi kuwona ndendende basi pamene cholakwika chiri.” Kenako, pamene Mzimu Woyera uwulula, kunena, “Dikirani miniti. Munachita *ichi* pomwe pano pa nthawi inayake *iyi*.” Izo zimakhazikitsa izo. Inu simungakane zimenezo. Mukuwona? Kunena, “Munachita *izi* apa.” Ndiye, ndiye izo zakonzedwa, inu mwawona. Tsopano, inu muyambire pamenepe. Mukuwona? Mwanjira imeneyo, zachitika.

297 Tsopano, inu mukudziwa kuti ine ndikuyankhula kwa inu ndi cholinga china. Ine ndakhala ndikulalikira. Mukuwona? Ndipo kenako ine—ine ndikungodzilowetsa ndekha—mu kudzoza kwa chinthu china, inu mwawona, kuwona ngati Mzimu Woyera ungabwere ndi kugwira ntchito pa ine ndi mphatso Yauzimu; ndiko kuti, zidziwitso ziwiri ziri pomwe pamodzi, zomwe zimandipatsa chisomo cha Mulungu kuti ndiwone masomphenya, ndi kuwona chimene chikuchitika, chimene chidzachitike, chimene chakhala chikuchitika.

298 Inu mukudziwa ngati izo ziri zoonu kapena ayi. Inu mwayima pano pamaso pa anthu osachepera faivi handirede, mwawona, kapena pafupi ndi iwo, firi handirede, mulimonse. Mukuwona? Ndipo—ndipo inu mukudziwa kuti izo—izo... Inu mukudziwa ngati izo ziri zowona kapena ayi. Ndipo—ndipo ngati ziri zowona, ndiye kuti ndi Mulungu. Baibulo linati, “Ngati pali mmodzi pakati panu, wauzimu kapena mneneri, ndipo chimene iye anena chichitika, ndiye mumvereni iye.” Mukuwona? Tsopano, “Ngati izo sizichitika, ndiye musamumvere iye.”

299 Tsopano, ine sindikudziwa chimene donayo wabwerera pamenepe. Koma tsopano mungolola Mzimu Woyera ubwere, ndipo muwone ngati Iye sanena izo. Mukuwona? Ndipo ngati icho sichingakhale chinthu chomwecho chimene Ambuye wathu anachita! Izo zingakhale zonse Iye angakhoze kuchita ngati Iye wayima pomwe pano, chifukwa, kumbukirani, ndi Iye. Ndi Iye. Si ine. Ine sindikumudziwa iye. Ine ndikuvomereza, sindikumudziwa iye. Chotero, izo zingatengere Iye.

Tsopano, ndithudi, donayo ali ndi kumverera kopambana ku mzimu wake.

300 Osati chifukwa iye wakweza dzanja lake mmwamba. Inu nonse mwakhala mmisonkhano, ndi kuwawona iwo akukweza manja awo mmwamba, kumachita monga *choncho*, ndipo Mzimu Woyera kuyitananso ndi kuwawuza iwo chimene iwo anali. Mukuwona? Uko nkulondola. Izo sizitanthawuza kalikonse. Kuwamva iwo akukuwa ndi kufuula; pomwepo, ukawawuza iwo pomwepo, “Iwe ukukhala ndi mkazi wa mwamuna *uyu*,”

ndinaziwona izo pomwe *apa*, ndi china chirichonse. Chabwino, inu mukudziwa. Inu mwakhala mmisonkhano ndi kuwona momwe zinthu zimenezo, ndi kuwona momwe zinthu zimenezo. Izo sizitanthawuza kanthu.

³⁰¹ Koma donayo akuwoneka kuti ndikumverera kodabwitsa kwa mzimu wake. Tsopano, donayo akuvutika ndi chinachake cholakwika. Ine ndikumuwona iye, momwe iye akudyera. Iye ali patsogolo panga tsopano, pa gome, ndipo akukhala ngati akudya kapena chinachake, zowoneka ngati chakudya chosamvetseka. Uko nkulondola. Kulondola uko? [Mlongo akuti, “Uko nkulondola.”—Mkonzi]. Ndiye kwezani mmwamba dzanja lanu kuti anthu awone izo. Mukuwona? Ine ndinamuwona donayo patsogolo panga, akuchita chinachake. Chirichonse chimene icho chinali, icho chiri pa tepi. Mukuwona? Chabwino. Tsopano, kuti inu mudziwe chifukwa chake. . . Iye ndi munthu wabwino.

³⁰² Penyani mphindi yokha. Tsopano Mzimu uli kudzoza. Tsopano, aliyense akhale molemekeza kwenikweni. Pitirirani kupemphera. Khalani mu pemphero, chifukwa ine ndinawona Iwo ukusuntha pa omvetsera pomwepo. Mukuwona? Tsopano khalani molemekeza kwenikweni.

³⁰³ Tiyeni timuwonenso donayo, kuti tingoyankhula naye. Chirichonse chimene Iye anakuwuzani inu. . . Eya. Ndi ichi apa. Ziri patebulo. Ndi—ndi vuto la mmimba. Ndi mtundu wina wonga matenda kapena chinachake mmimba. Dokotala wakhala akuyang’ana izi. Ndipo, titi, iwe wakhala ndi vuto ili kwa nthawi yayitali. Ndipo, kamodzi, ilo linanenedwa, “Chilonda, icho chikukwera.” Ndipo tsopano iye ananena chinachake. Chimenecho chinali chiyani? “Duodenum. Duodenum. Duodenum,” Ndinamumva iye akunena zimenezo. Mukuwona? Uko nkulondola. Ndiko kulondola ndendende. Dzina lanu ndi Abiti McCraw. Uko nkulondola. Pitirira tsopano, khulupirira ndi mtima wako wonse.

Iwe ukukhulupirira?

³⁰⁴ Mutatha kulira monga choncho, mutakhala kumbuyo uko, bwana, mapapo okugwa amenewo amene inu munali nawo mukuyenera kuti mumve bwinoko pakali pano, ngati mukukhulupirira. Zonse ziri bwino tsopano. Chabwino, izo zinachita izo. Ameni.

Kodi iye anagwira chiyani?

³⁰⁵ Mwamuna, pafupifupi awiri kumbuyo kwake apo, ndi kuwuma kwa mitsempha, ngati inu mukukhulupiriranso, bwana!

³⁰⁶ Kodi iye anagwira chiyani? Kodi inu simukuwona Kuwala uko kwapachikika pamenepo? Tayang’anani pa Chikasu icho *apo*. Ine sindikumudziwa mwamunayo, sindinamuwonepo iye mmoyo wanga. Mungowakhulupirira Ambuye Yesu.

307 Tsopano, penapake, pali khanda pano, khanda lili ndi khosi lopindika. Ndi izo apo. Ine sindikumudziwa iye. Khulupirirani, mlongo. Khosi la mwanayo liwongoka, ngati inu muti mukhulupirire izo.

Kodi iye anagwira chiyani? Aleluya.

308 Pali chinanso chokhudza khosi. Ine ndinawona icho. Ndi mkazi. Sindikutha kumupeza iye. Eya. Iye wakhala apa, akulira. Akazi a Riley, khulupirirani pa Ambuye Yesu Khristu, khosi lanu likhala bwino. Khulupirirani.

309 Ine sindikumudziwa mkaziyo. Sindinamuwonepo mmoyo wanga. Chinthu chokha chimene inu mukuyenera kuchita ndi kukhulupirira Yesu Khristu. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Khalani ndi chikhulupiriro.

310 Ine sindikukudziwani inu, bwana. Ndife alendo kwa wina ndi mzake, monga momwe ine ndikudziwira. Inu mukukhulupirira Yesu Khristu akhoza kundiwuza ine chimene vuto lanu liri? Inu mukudziwa ngati izo zingakhale zolondola kapena ayi, sichoncho inu? Ngati inu mungakhulupirire ndi mtima wanu wonse tsopano! Zikupitirira kupita kwa omvera. Inu mukukhulupirira kuti akazi anu kunjya uko akhala bwino, nawonso? [M'baleyo akuti, "Inde,"—Mkonzi]. Vuto la diso, iwo amavutika ndi vuto la diso. Mukukhulupirira izo? Inu siwochokera kuno. Ayi. Mukuchokera komwe kuli madzi ambiri, mwanjira yina. Ndi mzinda wa mmphepete mwa nyanja. Ndi California, Los Angeles. Bwererani, Bambo Bowman, ndipo mukhale bwino. Ndipo Yesu Khristu akuchiritsani inu.

311 Inu mukukhulupirira? Tsopano, inu, aliyense akhoza kuchiritsidwa pakali pano ngati inu muti mukhulupirire izo. Inu mukukhulupirira zimenezo?

312 Nanga bwanji inu mu mzere wa pemphero, inu mukukhulupirira izo, inunso? Inu mungokhala ndi chikhulupiriro, ndipo musakayikire. Khulupirirani ndi mtima wanu wonse, miniti.

313 Dona uyu, chifukwa chimene ine ndinayima ndi iye, ali movuto lalikulu. Mkazi uyu afa nthawi yomweyo ngati chinachake sichichitika kwa iye, chifukwa iye waphimbidwa. Mukuwona mthunzi wakuda umene uli pa iye?

314 Titi, inu mukudziwa, ife tiri ndi mthunzi wa imfa imeneyo pa anthu, wojambulidwa ndi kamera ya chithunzi, monga Mngelo wa Ambuye? Ife tiri nacho chitapachikidwa mu mpingo wathu; chinthu chachikulu kwambiri, chowoneka-chakuda, monga chimphelo, chikulendewera pa mkazi. Iwo anamuwuza iye kuti asajambule chithunzicho. Ndipo Mzimu Woyera unati, "Jambula pakali pano." Ndipo iwo anajambula chithunzicho, ndipo apo icho chinali. Mukuwona? Mbali zonse, apa. Icho chinapachikidwa kumeneko.

315 Inu anthu ochokera ku kachisi, ena a inu amene muli, amene muli pano, M'bale Fred ndi iwo, apa pali chinthu chomwecho chapachikika pa mkazi uyu.

316 Iye ali ndi khansa, ndiko kulondola, chikhodzodzo. Uko nkulondola. Ndi kulondola uko? Kwezani mmwamba dzanja lanu ngati izo ziri zowona. Mukuwona? Tsopano mdima wapita, opanda kunena kalikonse. Mwawona, chikhulupiriro chake chokha, icho chachita izo. Pitani, mukukhulupirira. Ameni. Ameni. Musakayikire izo. Mungopita ndi kukhulupirira ndi mtima wanu wonse.

317 Vuto la mtima limapha anthu ambiri, koma silingakupheni inu ngati mungakhulupirire. Ameni. Mungopita, mukuti, "Zikomo Ambuye." Pitani ndipo mukakhale bwino. Chabwino.

318 Mdierekezi akufuna kuti mukhale ndi nyamakazi iyi moyo wanu wonse. Koma ngati inu mukhulupirira ndi mtima wanu wonse, Yesu Khristu akuchizani inu. Inu mukukhulupirira izo? Yambani panjira yanu, kumuthokoza Mulungu.

319 Inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Inu mukhoza kupita kukadya chakudya chamadzulo chanu, ndipo vuto la mmimba limenelo likuchokerani inu. Mungopita ndi kuti, "Ambuye alemekezeke!" Pitani, mumukhulupirire Iye ndi mtima wanu wonse.

320 Inu munali, nanunso, vuto la mmimba. Khulupirirani ndi mtima wanu wonse, ndipo pitani, ndipo Yesu Khristu akuchizani inu. Chabwino.

321 Mukuchita mantha kwambiri ndi chiyani? Mukuvutika ndi manjenje. Zangotsala pang'ono kukugwetsani pansi, pafupifupi mu kuwonongeka, Satana akunama kwa inu. Koma izo zatha tsopano. Inu mukundikhulupirira ine? Pitani, ndipo munene, "Ambuye alemekezeke!"

322 Ambuye Yesu, ine ndikupemphera kuti Inu muchiritse mlongo wathu ndi kumupanga iye kukhala bwino, mu Dzina la Yesu. Ameni.

323 Bwerani, mukukhulupirira, mlongo. Mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikuyika manja anga pa iye chifukwa cha machiritso ake.

324 Bwerani, m'bale wanga. Mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikuyika manja anga pa m'baleyo kwa machiritso ake. Ameni.

325 Ndi angati ali ndi mtima wokhulupirira, pansi pa dzanja limene liti likwezedwe mmwamba? Tsopano ikani dzanja limenelo pa winawake pafupi ndi inu. Inu mukuti, "Kodi Amosi akananena zimenezo?" Iye ndithudi akanatero. Amenewo ndi Mawu a Ambuye. Inu mukweze dzanja lanu, inu mukhulupirire.

326 Yesu anati, "Zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene akhulupirira. Ngati iwo ayika manja awo pa odwala..." Sananene nkomwe kuti iwo adzawapempherera iwo. Anati,

“Ngati iwo ayika manja awo pa odwala, dzanja lokha litayikidwa pa iwo, iwo adzachira.”


Tiyeni tipemphere.

³²⁷ Ambuye Yesu, Mfumu yabangula ndi Liwu Lake, “Zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene akhulupirira. Ngati iwo ayika manja awo pa odwala, iwo adzachira.” Ambuye Mulungu, mulole chiwanda chirichonse chifuule. Mulole matenda aliwonse achoke. Mulole mdierekezi agonjetsedwe, ndipo ana a Mulungu atuluke mnyumba ino usikuuno mu chigonjetso ndi mphamvu ya chiwukitsiro cha Yesu Khristu.

³²⁸ Khulupirirani izo. Uko nkulondola. Mungokhala ndi izo. Nenani, mungoyika, ikani dzanja lanu pa winawake, mukuti “Ambuye, achiritseni iwo.” Ine ndikufuna kuti inu mupemphere. Ine ndinapemphera. Ine ndikufuna kuti inu mumupempherere winawake. Ndinu—ndinu. . . Ndinu Mkhristu monga ine ndiriri. Ife tonse ndife Akhristu. Tsopano inu mumupempherere winawake. Iwo akukupemphererani inu.

³²⁹ Tsopano, inu mungafune bwanji kuti winawake akupemphererani inu? Inu muwapempherere iwo monga inu mukufunira kuti winawake akupemphererani inu. “Chitirani kwa ena, inu mukanafunira kuti ena akuchitireni inu.” Pempherani kumene, khalani owonamtima, monga momwe inu mukufunira kuti iwo akukupemphererani inu.

³³⁰ “Ndipo pemphero la chikhulupiriro lidzapulumutsa odwala. Mulungu adzawaukitsa iwo. Ndipo ngati iwo akhala ndi kusakhulupirira kulikonse, iko kudzachotsedwa kwa iwo.” Chifukwa? “Mfumu ikubangula. Ndani amene sanenera? Ndani amene angachitire umboni pamene Mfumu yabangula?” Mawu Ake amati, “Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.”

M'bale Fuller, bwerani. Mulungu akudalitseni inu. 

63-0119 Njira Ya Mneneri Woon
Faith Temple
Phoenix, Arizona U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org